


MAFUNSO NDI MAYANKHO

AHEBRI GAWO I

 Iye akanachita bwanji izo popanda Mulungu? Izo zikanakhala zenizeni, sichoncho izo? Sizikanatheka popanda Ambuye.

Ine sindilalikira kuchokera kwa onse a iwo. Koma ndinaganiza kuti ndipeze chinachake cholemererapo, inu mukudziwa, chotero kulibwino ndizikonzekera. Koma, oh, iwo anali kwambiri, opepuka kwambiri. Chotero mwinamwake palibe mafunso ambiri pakati pa anthu ndiye, ndi mafunso ophweka ndi opepuka. Chabwino, ndine wokondwa kuyesera kuwayankha iwo mopambana momwe ine ndingathere, mothandizidwa ndi Ambuye.

² Ndipo ngati Mlongo Arganbright ali muno usikuuno... Mlongo Ruth. Kodi inu muli pano, Mlongo Ruth? Cha apa. Ine ndiri ndi... Oh, inde, ine ndiri ndi adiresi apa, ndipo... Ayi, ine ndiribe. Chabwino, ine ndikhoza kuyipeza iyo apa. Ine ndinali nayo mu bukhu la m'thumba langa, ndipo ndasiya bukhu la m'thumba langa kunyumba. Tsopano, ngati apolisi andigwira ine ndikupita kunyumba, M'bale Fleeman, inu mubwere mudzandipulumutse. Mumuuze Billy ine... ndasiya bukhu la m'thumba langa kunyumba, ndikuyendetsa wopanda laisensi usikuuno. Ndipo ndinaganiza kuti ndinali nalo m'thumba mwanga; ine ndinangosintha zovala. Ine ndinathamangira muno, madzulo ano, ndimadula udzu mwaliwiro ndithu ndipo ndimayenera kusiya ndi kuthamanga ndi kudzalowa muno, kusintha zovala ndi kuthamangira kumusi kuno. Ndipo ine—ine ndabweretsa la lexicon, koma mukhoza kutenga izo molondola kuchokera pamenepo.

³ Musamverere moyipa za kalata *imeneyo*. Ngati ine ndikanakhala kuti sindinapeze ina yoipa kuposa imeneyo, iyo ikanakhala kalata yabwino. Imeneyo inali yabwino. Iyo inali kwambiri, yabwino kwambiri. Ine ndinakuuzani inu kuti sindiwerenga iyo, koma ine ndinazembera pa iyo, inu mukudziwa, ndipo sindinathe kuzigwira izo motalika. Ndinangodabwa zomwe inu mumanena. Ndipo iyo inali kwambiri, yabwino kwambiri, yolembedwa monga momwe mphunzitsi weniweni amayenera kulembera. Iyo inali yabwino, ndipo ine ndikuyamikira zimenezo. Ndipo iyo—imakupatsa iwe...

⁴ Inu mwaona, ndimakonda makalata a winawake amene anga—angatsutsane nawe pang'ono. Mwaona, ngati

ungamapitirire nazo nthawi zonse, wopanda wina wotsutsana nawe, iwe umawuma. Iwe umayenera kukhala ndi kutsutsidwa pang'ono kuti uzimvetse ndi kukakumba mwakuya. Ndipo—ndipo iwe umangolowa mu vuto limodzi ngati sukusamalitsa; ndiye iwe—ndiye iwe umakhala mu vuto pamene uchita zimenezo. Ukuyenera kungokhala ngati ukumapitirirabe ndi kumupeza winawake woti azikutsutsa iwe. ndi kukufwanyula nthenga zako kamodzi panthawi.

⁵ Ku Afrika ine ndinapeza mikango iwiri yaying'ono, ndipo iyo inali tinthu tating'ono, pafupifupi monga *choncho*. Mkango, wawung'ono, wamangamanga; mkango wawung'ono, mkango waukazi wawung'ono. Ndipo tsopano, iyo inkawoneka ngati amphaka aang'ono, iyo inali yaying'ono kwambiri monga choncho, yaying'ono. . . tinthu tating'ono tokongola kwambiri, ito timangosewera. Ndipo ine ndinali woti ndiyibweretsanso iyo ku Amerika, ine ndinayika iyo mu khola la mbalame. Ine ndinali woti ndiyibwezeretsa iyo, koma sindinapeze chirichonse—chirichonse kuti ndiyipatse katemera iyo, chiphe chirichonse. Ndipo sakanandilola kuti ndiyibweretse iyo ku United States popanda iyo kupatsidwa katemera poyamba, ndipo sindinamupeze mu Africa monse. Koma ngati mukanafuna kudziwa ngati iwo unali mkango kapena ayi, mungowumanga iwo mmbuyo pang'ono pokha. Iwo umangopanga ukali ndikukudziwitsani kuti iwo ndi mkango, chotero—chotero izo zikukudziwitsani inu pamene iye anayima.

⁶ Umo ndi momwe iwe umayenera kuchitira kamodzi mu kanthawi, inu mukudziwa, kukhala ngati kukankhira nthenga chammbuyo, kuti udziwe. Koma, tsopano, ife sitimakwiya monga mkango; ife basi—ife timangozikonda izo, kuli. . . anthu azifunsa mafunso. Ndipo mafunso ngati amenewo, Mlongo Ruth, ndi kwambiri, wabwino kwambiri kwa ine. Ndi a. . . Ine—ine ndikuzikonda zimenezo, mwaona. Ndi mtundu woyipa kwambiri umene ndimadana nawo kuwutenga. Koma iwo ndi a. . . izo zinali zabwino.

⁷ Tsopano ife tiri nawo ena abwino, okondoweza, mafunso apakhomo basi. Kuli mlaliki kumbuyo uko kumbuyo kwa chipinda pakali pano, anandifunsa ine, anati, “Aneneri awiri a Chivumbulutso 11, kodi iwo adzabwera Mkwatulo usanachitike? Kapena kutengedwa kwa Israeli kusanachitike? Ndipo chiyani. . .” Tsopano, ndiwo mtundu wa mafunso amene—amene—amene amakumangirira iwe mozungulira. Koma mafunso ophweka ngati awa ndi abwino.

Koma tsopano, ife tisanayambe, tiyeni tiweramitse mitu yathu kwa pemphero.

⁸ Atate, zadziwika kuti pamene Inu munali usinkhu wa zaka thwelofu, Inu munapezeka muli mu Kachisi limodzi ndi alembi ndi anzeru, mukukambirana ndi iwo Malemba. Ndipo iwo

anali—iwo anazizwa ndi a . . . anthu akale, ndi ophunzitsidwa bwino m'Malemba, ndipo komabe kumuwona Mnyamata wamng'ono wa pafupifupi usinkhu wa zaka thwelofo basi akukhoza—akungododometsa, mu kufotokoza kwa Malemba. Inu munali pa ntchito ya Atate Anu. Inu munanena kwa amayi Anu, “Kodi inu simukudziwa kuti Ine ndikuyenera kukhala pa ntchito ya Atate Anga?” kufotokoza Malemba ndi kutanthauzira kwake kwauzimu.

⁹ Ndipo tsopano ife tikupemphera, Ambuye, kuti—kuti Inu mukudziwa momwe ife tiriri ofooka ndi otopa, ndi momwe ife tiriri akuti timalakwitsa, kuti Inu mungobwera ndi ife usikuuno mmawonekedwe a Mzimu Woyera, ndipo mudzawafotokoze Malemba kwa ife. Ine ndikudikirira ndipo ndikudalira pa Inu. Ndipo ngati ndingadzatero, pa nthawi iliyonse, kudzayesera kuikapo maganizo anga kapena kutanthauzira kapena chinthu china chodzikhonda, kudzayesera kuzipanga izo kuti zimveke monga momwe ndimafotokozera izo kuti zikhale bwino, mudzatseke kamwa yanga, Ambuye, monga Inu mungachitire . . . Inu munachitira ndi mikango, pamene iyo inabwera kwa Daniele. Inu mukadali Mulungu yemweyo.

¹⁰ Ndipo mulole izo zikhale kwathunthu . . . Pamene ife tikudalira pa Mzimu Woyera, mulole Iwo ungowululira zinthu izi kwa ife. Ndipo kenako pamene Iye aziyankhula izo, muzipange izo zimveke bwino mwakuti amene anafunsa funsola akhoze kuwulandira Iwo. Ndipo ngati Iwo ungayankhe motsutsana ndi zomwe ine ndakhala ndikuzikhulupirira nthawizonse, ndiye mulole mtima wanga ukondwere nawonso, Ambuye, kudziwa kuti ndapeza chinachake chatsopano, ndi njira ina yabwino ya Ambuye. Pakuti Inu munati, “Fufuzani Malemba, pakuti mwa Iwo inu mukuganiza kuti inu muli nawo Moyo Wamuyaya, ndipo Iwo ndi Amene akuchitira umboni za Ine.”

¹¹ Tsopano, tikamalizitsa kuphunzitsa kwa Lemba uku, izo ndithudi ziwutsa malingaliro ambiri ndi zina zotero. Ndipo ine ndikupemphera, Mulungu, tsopano kuti mafunso onsewa akuwoneka kuti akufunsiidwa mokoma ndi modekha, mulole Mzimu Woyera modekha ndi mokoma uwayankhe iwo. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu, ndi kwa ulemelero wa Mulungu, ndi kumangirizika kwa Mpingo Wake. Amen.

¹² Pali nthawi zambiri zimene zolinga zodzikonda kwa chirichonse, zimangowononga kukoma konse kwa izo. Ndipo tsopano, mafunso pambuyo pa Lemba ili afunsiidwapo.

¹³ Tsopano, ngati ine ndingapange phokoso pang'ono pokha usikuuno, ine ndachotsa dzino. Ndipo ndikalibwezeretsa ilo, ndipo ine sindingalalikire, ine ndimachedwa pamene ine ndikulalikira; ndikalichotsapo ilo, ndipo ndimatsala pang'ono kuyimba mluzu.

¹⁴ Akazi a Billy Graham ananena nkhani ya iye, kuti chosangalatsa choyipa chomwe iye anayamba wamuwonapo iye, chinali, iye ali ndi dzino lotuluka patsogolo. Ndipo iye analitaya ilo, ndipo iye anali ndi programu ya pa televizioni nthawi yomweyo, ndipo—ndipo samatha. . . Ilo linali m’mbale ndi ndi mano ena akumbuyo ali mmenemo. Ndipo pamene iye ayamba kuyankhula, iye amaliza mluzu “psyii, psyii” kumadutsa pa dzino lake. Ndipo iye anati iye anali atagwada pa maondo ake, akupemphera ndi kutuluka thukuta, maminiti teni asanayambe kuwonetsa pa televizioni, ndipo pamapeto pake iwo analipeza ilo pamene ilo linagwera kuchokera mu thalauza lake ku mapazi a nsapato zake. Mmodzi wa othandizira analipeza ilo, dzino lonyengera lija. Ndipo Akazi a Graham anazinena izo pa iye, ndi cha apa. Ndipo chotero ine ndinaliyika ilo mu kachidutswa kakang’ono ka pepala, ine ndikuganiza ine ndiri nalo ilo pomwe pano mu Baibulo langa.

¹⁵ Ndipo chotero izo ziri ngati. . . pamene ife tikalamba pang’ono ndi kufooka, inu mukudziwa, ndi kumataya izi, izo zimapangitsa izo kukhala zoyipa. Ndipo chotero ine. . . pamene ine ndinali uko ndi M’bale Roberson kumbuyo uko, ndi iwo, ine ndinali kulipukuta ilo mmawa wina ndipo ndinakhobola chidutswa pa ilo, ndipo ine ndinachita kulitengera ilo kwa adokotala, kuti akalikonze ilo. Kotero Ambuye awonjezere madalitso Ake.

¹⁶ Tsopano ife tikupita, tsopano, ine ndiyetsa kuti ndidutse mu lirilonse la iwo, ngati ine ndingathe. Ndipo, M’bale Tony, mwa chisomo cha Mulungu, ine ndapeza kutanthauzira kwa loto lanu, ndipo ilo linali lodabwitsa. Ndine wokondwa kuziwona izo. Ndipo ndi kutanthauzira kwabwino, komwe ndikuganiza kuti sindikuyenera kukupereka pagulu pano, chotero ndikupatsani inu mwapadera ngati inu—ngati inu simu. . . ngati mukufuna izo mwanjira imeneyo. Iye anandifunsa ine usiku wina, iye anali ndi loto, ndipo ine sindikanamuza iye basi chomwe ilo linali mpaka ine nditapita kwa Ambuye ndi kukapempherera ilo. Kenako Ambuye anawulula izo kwa ine ndipo anandiuza ine chimene kutanthauzirako kunali. Ndi zodabwitsa, ndi nkhani yabwino kwa inu, M’bale Tony.

¹⁷ Tsopano, mu funso loyambirira. Tsopano, ine sindikudziwa basi pamene ndingayambire, chifukwa iwo onse ndi abwino. Koma, tsopano, ife tiyetsa kuti tisatalikitse kwambiri, ndipo mwinamwake ife tikhoza kudzamaliza iwo Lamlungu, ngati ife sitiwamaliza iwo.

51. Tafotokozani chimene chimatanthauza pa “chilango chosatha,” mu Mateyu 25:46. “Koma a . . .” Ndiro funsolo.

52. Kenako, funso lachiwiri: “Koma ana a ufumu adzaponyedwa ku mdima wakunja,” kodi izo ndi

chimodzimodzi ngati kuwachotsa iwo m'maganizo a Mulungu?

¹⁸ Chabwino, tsopano, nditenge funso lanu loyamba, limene likupezeka mu Mateyu Woyera-... mutu wa 25. Tsopano ife ti... Tsopano, ine sindinawerenge izi, ndinangoyang'ana pa izo kumbuyo uko, ndipo ndinangoyesetsa mwakukhoza kwanga kuti ndiziyang'ane izo mopambana momwe ine—momwe ine ndinadziwira kutero. Ndipo wanga... Inu mutsegule nane mu Mabaibulo anu, pamene tikuwerenga Ilo. Tsopano, ine ndimafuna kuti nditenge izi kuchokera mu lexicon ya Chigriki aponso, kuchitira kuti mumvetse—zapachiyambi za izo. Ndipo ine—ine ndikuzikonda zimenezo. Ndiyeno ife tikhala nawo Iwo mu ziwiri zonse—mu ziwiri zonse—Chigriki ndi linalo. Ndipo tsopano izi zikhala—zikhala ngati zochedwerapo, ndi kuphunzira, chifukwa ine ndikuyenera kufikira ndi kukagwira Malemba paliponse pamene ine ndingawapeze iwo, ndi kuwatengera iwo pamalo awo. Chabwino.

¹⁹ Tsopano, alipo amene akufuna Baibulo kuti aziwerengamo? Ngati inu mukutero, kwezani dzanja lanu mmwamba. Ndipo ife... Ine ndikuganiza tiri nawo atatu kapena anayi kumbuyo kuno. Ngati inu mukufuna kuwerenga mwa Lemba, chabwino. M'bale Cox, kodi mungabwere kuno ndi kudzanditengera Mabaibulo awa? Ndipo izo—izo ndi zabwino kwa inu, ngati inu mungathe, kuti... (pali mmodzi, ndipo inu basi—inun mungowatengera iwo kumeneko ngati inu mukufuna kutero, ochuluka chomwecho). Ndipo aliyense amene akufuna limodzi, mungokweza dzanja lanu mmwamba, mnyamatayo abweretsa ilo kwa inu pomwepo, mwaona. Ndipo ife tikufuna kuti tiphunzire izi limodzi, ndipo basi... .

²⁰ Tsopano, pa kuwerenga uku ndi mitu yotsiriza... mitu seveni yoyamba ya Bukhu la Ahebri. Tikatha kuphunzitsa, ndithudi, mnyamata amene analemba izi, maphunziro awa, M'bale Mercier ndi M'bale Goad, ali nazo izo ndipo tsopano akukonzekera kuti azisindikize izo m'bukhu. Ndipo iwo ali nazo izo. Tsopano... ndipo tiribe chirichonse choti chapesedwa mwaheka, ife tangopalapasa pamwamba. Ndipo ine ndikuganiza iwo anadzitcha izo... ndipo atenga—zonona kuchokera mu... ndipo nkumangopukuta zononazo, zonona zapang'ono chabe za kuphunzitsa kwa Ahebri. M'bale Mercier akhala nazo posachedwapa, zitasindikizidwa, aliyense amene akuzifuna izo.

²¹ Tsopano izi mkati umu, izo zikubweretsamo... Inu simungathe kudutsa basi... mu mpingo wauvangeri, chimene uwu ndi mpingo wauvangeri. Inu simungadutse mu a—chiphunzitso popanda kudzutsa kukayikira ndi maganizo a anthu ambiri. Inu mukuyenera kutero. Tsopano, ine ndiri kutali kuti ndingakhale mphunzitsi, osati wolifotozoza Baibulo nkomwe. Koma ine sindimayesera nkomwe kuti—kuti ndinene

chirichonse, kapena kuti ndichite chirichonse, koma choyamba—choyamba ndimafunsa kapena kufufuza chinthu chabwino changa cha izo.

²² Zinafunsidwa za ine ndi m'bale wokonedwa, usiku wathawu, iye anati, “M'bale Branham, M'bale Seward nthawi ina ananena kuti iwe—iwe sungathe kukupanikizani inu paliponsepo. Mwaona, kuti inu nthawizonse mumakhala ndi njira ina yoti mutulukire kwa izo kapena kuchoka kwa izo.”

²³ Ine ndinati, “Chabwino, chifukwa cha izo, ine nthawizonse ndimayesetsa kuti ndiganize ndisanachite chirichonse. Mukuona? Ndiyeno ngati anthu andifunsa ine, ndiye ine ndikhoza kuwauza iwo chimene maganizo anga anali. Mukuona?” Koma izo zimatheka ngati ukuganiza molondola. Ndipo iwe usanachite chirichonse, uziyesera kutenga mbali imene Mulungu akadafuna kuti iwe utenge, ndiye izo ndithudi zingakhale zovuta kuti ufinyidwire pansi.

²⁴ Inu simungalingalire nthawi imene—imene Ahabu anayesetsa kuti amufinyire Eliya pansi. Kodi inu mungalingalire nthawi imene Afarisi anayesera kumufinyira Yesu pansi? Mwaona, Iye anali—Iye amakhala ndi yankho mwamsanga, chifukwa chirichonse chimene Iye ankachita, Iye ankachita icho mwa chifuniro cha Mulungu, ndipo Iye . . . umo ndi momwe Iye—Iye akanakhoza kupezera izo. Tsopano, umo ndi momwe ife tikuzifunira izi mwa momwemo.

Tsopano funso likufunsidwa, ife tilisunga funsolo:

Tafotokozani chimene chimatanthauza ponena kuti “chilango chosatha,” mu Mateyu 25:46.

²⁵ Tsopano mvetserani mwacheru kwenikweni. Aliyense tsopano, Mateyu 25:46:

Ndipo awa adzapita ku chilango chosatha: . . .

²⁶ Tsopano, funsolo likuti, “Chiyani . . . Tafotokozani . . .” Tsopano mawu oti *chosatha* amachokera ku mawu oti kuchokera “zonse ndi nthawizonse,” ndi *kwanthawizonse* “danga la nthawi.” Izo zimangotanthauza “nthawi yochuluka chomwechi,” monga *kwanthawizonse*. Tsopano ngati mungati mungowerenga . . . Ine sindikumudziwa amene analemba mafunsowa, chifukwa palibe amene wayika dzina lake pa iwo; izo sizimasowa kutero, ine sindikuwafuna iwo, mwaona.

Koma awa adzapita mu chilango chosatha: . . .

(Tsopano penyani, amenewo ndi oyipawo.)

²⁷ Tsopano, wokonedwa—munthu wokonedwa amene anafunsa funsolo, tangowerengani zonse za Iwo:

. . . koma olungama ku moyo wamuyaya.

²⁸ Oyipa adzapita ku chilango chosatha (kadanga kenakake ka nthawi), koma olungama ali nawo Moyo Wamuyaya. Inu

simudzachipeza konse chilango Chamuyaya, sizingatheke konse. Mwaona, ngati iwo angakhale ndi chilango Chamuyaya, iwo ali ndi Moyo Wamuyaya; iwo ali ndi Moyo Wamuyaya, iwo apulumutsidwa. Mwaona, izo sizingatheke. Tsopano ngati mungayang'anitsitse, a—funsolo linadzifunsa lokha... likudziyankha lokha. Mukuona?

Ndipo awa...

Tsopano penyani, ine ndifika apa:

...ndipo *owo*...

29 Mu ya 20...Ndime ya 44:

...ndipo *owo nawonso* anayankha, anati kwa Iye, *Ambuye, ndi liti* limene ife tidzakhale ndi *njala*, ndi liti tinakhala ndi ludzu, ndi *mlendo*, ndi *wamaliseche*,... ndi *mu ndende*, *ndipo sanatumikire kwa inu*?

Kenako adza—kenako iye adzawayankha iwo, kuti, Indetu Ine ndinena kwa inu, Mochuluka *momwe inu munachitira* izo...kwa *mmodzi wa aang'ono awa*, inu *munachitira* izo...kwa *ine*.

Ndipo awa adzapita ku chosatha (chosatha) chilango: (amenewo ndi oyipa)...*koma olungama ku Moyo Wamuyaya*.

30 Mukuona kusiyana kwake? Oyipa ali ndi chilango chosatha, koma *chosatha* ndi “danga la nthawi.” Tsopano, ngati izo zikanakhala zofanana, izo bwenzi zitalembedwa, “Ndipo awa adzapita ku chilango chosatha, enawo adzapita ku moyo wosatha.” Mukuona? Kapena, “Iwo adzapita ku chilango Chamuyaya, ndipo enawo ku moyo Wamuyaya.” Mwaona, ngati kuli chilango Chamuyaya, kuti adzalangidwa kwanthawi zanthawi, ndiye kuti ndi Amuyaya... ali ndi Moyo Wamuyaya; ndipo Moyo Wamuyaya umodzi wokhawo, ndipo umenewo umachokera kwa Mulungu. Chirichonse chopanda chiyambi chilibe mathero, chirichonse chimene chiri ndi chiyambi chimakhala ndi mathero. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

31 Tsopano, Lemba Palokha limene—munthu wokonedwa anayankha... Tsopano ngati mungazitenge izo mu lexicon, “*Ndipo awa adzakalowa mu ainion, kukadulidwa, ndi kukalowa mu wosa...ndi ku moto, nyanja ya moto.*” Tsopano, mawu akuti *a-i-n-i-o-n* amatanthauza “danga la chilango.” Mu lexicon ya Chigriki, pomwe apa, “danga la chilango,” kapena, “nthawi ya chilango.” Taonani, “Iwo adzapita ku nthawi ya chilango.” Mawu amene akugwiritsidwa ntchito, *a-i-n-i-o-n*. *Ainion*, amene akutanthauza “nthawi, nthawi, nthawi yamalire.” Ndiye muzitengere izo kubwerera mu—mu kumasulira apa, Chingerezi, *chosatha* ndi “nthawi yamalire.” Mwaona, iwo akuchokera ku

Chigriki, “malire a nthawi.” Mawu akuti *ainion*, kapena *a-i-n-i-o-n*, *ainion* amatanthauza “nthawi yamalire ya chilango.”

³² Komano werengani enawo, “Koma awa adzapita ku Muyaya.” Ndiko kusiyana kwake. Mwaona, Moyo Wamuyaya. *Wamuyaya* amachokera ku mawu akuti “Umuyaya,” ndipo Umuyaya unalibe chiyambi kapena mapeto. Ndi kwanthawi za nthawi. Tsopano izo zikuyenera kuyankha zimenezo, mwaona, chifukwa ngati inu mungawerenge Lemba mwatcheru kwenikweni, inu muwona.

³³ “Ndipo awa adzapita ku chilango chosatha, koma *olungama...*” Oyipa adzapita ku chilango chosatha, nadzalangidwa kwa danga la nthawi; mwinamwake zaka billioni, ine sindikudziwa, koma inu ndithudi mudzalangidwa chifukwa cha machimo anu. Koma motsimikiza basi monga momwe tchimo linali ndi chiyambi, tchimo liri ndi mathero. Chilango chinali ndi chiyambi, ndipo chilango chidzakhala nawo mathero. Ndipo gehena inalengedwera mdierekezi ndi angelo ake. Mukuona? Chabwino. Tsopano, ine ndiri ndi lina pansi apa loti ndiyankhire mu zimenezo, basi mu maminiti pang’ono, lomwe liri lokongola, kumangiriza mwa ilo.

Tsopano, koma awa apa: **“Koma ana a ufumu adzaponyedwa kunja mu mdima,” kodi izo ndi chimodzimodzi kuwaponya iwo m’aganizo a Mulungu?**

³⁴ Ayi, izo sizingakhale zofanana. Tsopano, inu mukulozera apa ku Mgonero wa Chikwati. Tsopano, “Ndi ana a ufumu,” monga anafunsidwa apa. Ana a ufumuwo ndi Ayuda, ndipo anaponyedwa ku mdima wakunja. Ndipo iwo—iwo aponyedwa mu mdima wakunja, ndipo iwo adutsa mu nthawi ya kulira ndi kuisima ndi kukukuta kwa mano. Iwo anaponyedwa mu mdima wakunja chifukwa izo zikanakupatsani inu ndi ine mpata kuti tilape, koma iwo sanachotsedwe konse mmalingaliro a Mulungu. Iye sadzaiwala konse Israeli. Ndipo Israeli, monga wowerenga Baibulo aliyense amadziwira, amanenedwa ngati “ana a ufumu.” Mwaona, ndi ufumu, lonjezo. Mwa kuyankhula kwina, Mulungu akuchita ndi fuko, pamene Iye ankachita ndi Israeli, amene ali ana a ufumu.

³⁵ Tsopano, inu mukukumbukira, Iye ananena pamenepo, “Ndipo Abrahamu ndi Isaki ndi Yakobo,” pamalo amodzi, “adzabwera ndi kudzakhala mu ufumu pa nthawi yotsiriza.” Mwaona, ndipo kuti Abrahamu, Isaki ndi Yakobo adzakhala mu ufumuwo; iwo anali, iwo anali anthu odalitsa ufumu. Koma ana a ufumu adzaponyedwa mu mdima wakunja.

³⁶ Tsopano, pamene zonedwazo zikuchokerapo apa ndi—ndi Mkwati. Pamene Mkwati anabwera, pamene iwo anali... Asanu a anamwaliwo anapita kukakumana ndi Ambuye, ndipo—ndipo sanatenge mafuta aliwonse mu nyali zawo. Ndipo a—asanu enawo anatenga mafuta mu nyali zawo.

Tsopano, ngati mungazindikire, ndi chithunzi chokongola, awiri onse Myuda ndi Wamitundu, monga okanidwa. Kumbukirani kuti, pali magulu atatu a anthu nthawi zonse: Myuda, Wamitundu (okhazikika), . . . ; Myuda, Wamitundu, ndi Mpingo. Ngati muwasakaniza amenewo, inu ndithudi mudzakakhala mu vuto pamene mudzafike ku Chivumbulutso. Pakuti ngati inu simudza . . .

³⁷ Monga Bambo Bohanon ananena kwa ine nthawi ina, anati, “Billy, aliyense amene angayesere kuwerenga Chivumbulutso akhoza kulota zilubwelubwe. Bwanji,” iye anati, “apa pali Mkwatibwi pansi apa pa dziko lapansi, ndipo—ndipo chinjokacho chikulavula madzi kuchokera m’kamwa mwake kuti chikapange nkondo ndi Iye.” Ndipo anati, “Ndiye nthawi yomweyo imene Mkwatibwi wayima ngati handiredede ndi forte foro sauzande” (Chiphunzitsa cha Mboni za Yehova) “pa Phiri la Sinai. Ndipo nthawi yomweyo Mkwatibwi ali Kumwamba.” Ayi, ayi, inu mukulakwitsa.

³⁸ Pali magulu atatu a anthu. Mwaona, amenewo ndi, Myuda wokanidwa, ndipo pali namwali wogona amene madzi . . . Si Mbewu ya mkazi, ndi wotsalira wa Mbewu ya mkazi amene chinjoka chinalavula madzi kuchokera m’kamwa mwake . . . Chivumbulutso 11. Ndiyeno, kwenikweni, Ayuda handiredede ndi forte-foro sauzande sanali mwamtheradi Mkwatibwi, iwo ndi otsalira a mpingo wa Chiyuda. Ndipo chiphunzitsa cha Mboni za Yehova chimene chimawayika iwo ngati Mkwatibwi, ine sindikuwona momwe inu mungachitire zimenezo, chifukwa, si Mkwatibwi.

³⁹ Ngati inu mungazindikire mu Chivumbulutso uko, Ilo linati, “Ndipo iwo ndi anamwali.” Ndipo iwo ndi adindo. Ndipo mdindo anali chiyani? Iwo anali . . . Mdindo anali olondera mkachisi amene ankamulondera mfumukazi, chifukwa iwo anali . . . chi- . . . Iwo anali amuna amene anafulidwa. Iwo anali . . . Kodi inu munazindikira, anati, “Iwo anali oti sanadziditse okha ndi akazi?” Iwo anali adindo a mkachisi. Ndipo chinali chiwerengero chosankhidwa chimene Mulungu anachichotsa kuchokera mwa osankhidwa a Ayuda. Tsopano, ngati inu mungazindikire . . . Ngati ife titangozitunga izo mphindi chabe, kuti izo zikhale ngati zikukhazikitsa izo mmalingaliro anu, pamene inu mungathe kwenikweni . . .

⁴⁰ Tiyeni titenge Chivumbulutso, mutu wa 7, ndipo ife tidzapeza apa tsopano, kuti . . . zomwe Iwo ananena. Ndi chinthu chokongola:

Ndipo zitatha izi . . . Ndinawona angelo anayi atayima pa ngodya zinayi za dziko lapansi, . . . (tsopano, izi zikufanana ndi Ezekieli 9, pamene iye anawona chiwonongeko cha Ayuda. Ndipo apa iye akuwona chiwonongeko cha Amitundu, Chivumbulutso,

mutu wa 7) . . .Ndipo *ndinawona angelo anayi atayima pa ngodya zinayi za dziko lapansi, atagwira mphepo zinayi (mphepo zimatanthauza “nkhondo ndi mikangano”)* . . .*kuti mphepo isawombe pa dziko lapansi, kapena pa nyanja, . . .kapena mtengo uliwonse. (ndipo imeneyo ndi nkhondo, “kugwira”)*

⁴¹ Oh, ife tikanakhala ndi nthawi yoti tipite mwatsatanetsatane pa funso ili. Zimenezo zinachitika. . . Pamenepo ndi pamene Russell anasokonezeka. Russell analosera, anaziwona izi zikubwera. Iye analosera “kudzakhala Kudza kwa Ambuye Yesu,” osadziwa kuti iko kunali—kusindikizira kutali kwa Mpingo. Mukuona?

⁴² Ndipo iwo amadabwa mmene nkhondo yapadziko lonse. . . Nkhondo Yoyamba Yapadziko Lonse. Penyani, iyo inatha pa Novembara leveni, pa leveni koloko tsikulo; mwezi wachi leveni, tsiku lachileveni, ndi ora lachileveni. Ndipo mwachangu zitachitika zimenezo, ubatizo wa mmadzi mu Dzina la Yesu unawululidwa ndi Ubatizo wa Mzimu Woyera kwa Mpingo. Ndendende, mwamsanga zitangochitika zimenezo.

⁴³ Ngati mungazitengere izo mu Chivumbulutso, momwe tinazimangirizira Izo pamodzi, ndipo pakati pa M’badwo wa Filadelfia ndi Laodikaya. Ndipo Amethodisti anali ndi M’badwo wa Filadelfia, chikondi chapabale. Ndipo m’badwo wotsiriza, m’badwo wa mpingo, unali M’badwo wa Laodikaya, umene unali m’badwo wofunda. Ndipo Iye ananana pamene, “Ndayika khomo (khomo lotsegula) patsogolo panu.” Khomo lotsegula! Ndipo ngati mungalozere ku Malemba amenewo, iwo adzamangirizira Uthenga wonsewo pamalo amodzi apo, kuti akuwonetseni inu ndendende.

⁴⁴ Penyani! Apa kuti chirichonse chinali Atate, Mwana, Mzimu Woyera, mu ubatizo, (chimene ife tikuyenera kulowamo molunjika) chimene chinali mwamtheradi kachikhulupiriro ka Chikatolika ndipo osati chiphunzitso cha Chikhristu. Ayi, bwana. Ine basi. . .Ife tiri nazo izo pomwe pano, usikuuno, kuti tibwere mu zimenezo; ndi lexicon, nayenso. Mukuona? Inde, bwana, ndi mbiriyakale nayonso. Panalibe aliyense amene anabatizidwapo monga choncho mu Baibulo, kapena osati kwa zaka sikisi handiredi zoyambirira Baibulo litabwera. Ndipo ndikhoza kutsimikizira izo pomwe pano mwa chiphunzitso cha Chikatolika chomwe, kuti iwo ndi amene anayambitsa izo, ndi kukonkha ndi kuthira.

⁴⁵ Izo zinatuluka mmenemo kupita ku mpingo wa Chiwesile, ndi ku mpingo wa Methodisti, Amethodisti anabweretsa icho mpaka kwa Abaptisti, Abaptisti anabweretsa icho mopitirira, ndipo icho chikadali chiphunzitso chabodza! Ndipo ndikhoza kubwerera mu Baibulo ndi kudzatsimikizira kwa inu kuti Baibulo linanena zimenezo “muli nalo dzina lakuti muli ndi

moyo, koma ndinu akufa.” Ndizo kulondola ndendende. Ndipo iwo anali . . .

46 Ine ndikhoza kutsimikizira kuti Baibulo linaphunzitsa kuti iwo akanadzagwiritsa ntchito Dzina Lake mu ubatizo mpaka mu m’badwo wa mdima, malingana ndi—m’badwo wachinayi . . . wa—m’badwo wa mpingo, M’badwo wa Mpingo wa Pergamo. Ndipo Iye anati, mu, mu zaka fifitini handiredi za mibadwo ya mdima zimenezo, aliyense, anati, “Inu mwatsala ndi kuwala pang’ono, chifukwa simunakane Dzina Langa.”

47 Pamene izo zinafika ku m’badwo wina uko, m’badwo wa Katolika, Iye anati, “Inu muli nalo dzina loti inu ‘muli moyo,’ koma ndinu akufa! Ndipo inu mwalikana Dzina Langa.” Ndi inu apo. Mukuona? Izo zonse zimangomangiriza chithunzi chimodzi chachikulu chokongola pamodzi, Baibulo lonse.

48 Tsopano zindikirani ichi:

. . . atazigwira mphepo zinayi . . .

*Ndipo ndinawona mngelo wina akukwera kuchokera
Kumwamba, ali ndi chisindikizo cha Mulungu
wamoyo: . . . (Chisindikizo)*

49 Tsopano, kodi chisindikizo cha Mulungu wamoyo ndi chiyani? Tsopano, inu abale a Advent munena kuti, “Kusunga tsiku la sabata.” Ine ndikufuna inu mudiwonetse izo mu Lemba. Izo mulibemo mmenemo. Palibe malo amodzi amene anachita izo . . . ndi—ndi chisindikizo . . .

50 Ngati mungawerenge Aefeso 4:30, mwaliwiro ndithu, inu mupeza chimene Chisindikizo cha Mulungu wamoyo chiri. Aefeso 4:30 amati, “Musawukhumudwitse Mzimu Woyera wa Mulungu umene inu munasindikizidwa nawo mpaka tsiku la chiwombolo chanu.” Osati mpaka chitsitsimutso chotsatira, koma muli ndi chitetezero Chamuyaya (uh-huh). “Musawukhumudwitse Mzimu Woyera wa Mulungu umene munasindikizidwa nawo kufikira tsiku la chiwombolo chanu.” Muwone ngati Aefeso 4:30 sakunena zimenezo, ndiye mutenge zowerengera zanu za mmalire ndipo muziyendetse izo njira ina yonse kudutsa mu Malemba pamenepo, ndi kufufuza. Tsopano, “Kusindikizidwa mpaka tsiku la chiwombolo chanu. Kukhala ndi chisindikizo cha Mulungu wamoyo.”

51 Tsopano, kumbukirani, Mzimu Woyera sunaphunzitsidwe ngati Ubatizo wa Mzimu Woyera mpaka itatha Nkhondo Yadziko Yoyamba. Ife tangokondwerera kumene chathu—chisangalalo chathu chagolide, zaka forte, kapena chaka cha forte cha chisangalalo.

*. . . ndipo iye anafuula ndi mawu aakulu kwa
angelo anayi, kwa amene kunaperekedwa mphamvu
yowononga dziko lapansi kapena nyanja,*

Akuti, Musavulaze dziko lapansi, kapena nyanja, kapena mtengo uli wonse, mpaka ife titasindikiza antchito... (tsopano mukufika ku funso lanu, “ana,” mwaona)... *antchito a Mulungu wathu pamphumi pawo.* (musavulaze, musawononge dziko lapansi, musalole kuti bomba la atomiki liphulike, musakhale ndi chinthu chathunthu mpaka *antchito* a Mulungu wathu atasindikizidwa)

⁵² Tsopano, ngati ife tingazitengere izo mmbuyo umo ndi kuthamangira kumbuyo uko, momwe kuti—kuti ngakhale mu *The Decline of the World's War*, mu voliyumu yachiwiri, pamene General Allenby anamenya mpaka iye anafika pa mizere ya Yerusalemu, ndipo iye anangolumikizana ndi Mfumu yaku England, ndipo anati, “Ine sindikufuna kuwombera pa mzindawo, pa chifukwa cha kupatulika kwake.” Iye anati, “Ine ndichite chiyani?”

⁵³ Iye anati, “Pempherani.”

⁵⁴ Ndipo iye anawulukiranso pamwamba pake, ndipo pamene iwo anatero, iwo anati, “Allenby akubwera.” Ndipo munalii Achimuhamadi mmenemo, ankaganiza kuti iye anati, “Allah akubwera.” Ndipo iwo anakweza mbendera yoyera ndipo anadzipereka ndipo Allenby anapita ku Yerusalemu ndipo anakatenga popanda kuwombera chipolopolo, molingana ndi mauneneri, ndiko kulondola, ndipo anawubwezeranso kwa Ayuda.

⁵⁵ Kenako iwo anadzutsa Hitler kuti akawazunze Ayuda, ndi konse konse pa dziko lapansi, ndi kuwathamangitsira iwo kwawo kumeneko.

⁵⁶ Ndipo Baibulo linati Iye akanadza “wabweretsanso iwo pa mapiko a mphungu.” Ndipo pamene iwo anayamba kubwereranso... *Life* Magazini ndi iwo analemba izo masabata angapo apitawo, kumene iwo anawabweretsa iwo mma sauzande, kulowa mu Yerusalemu, ndipo iwo anapita kukawanyamula okalambawo pa nsana wawo. Iwo anafunsidwa. Ine ndiri nazo zonsezo pa gudumu ndi chithunzi. Ndipo iye anati... Apo panapachikika mbendera ya nyenyezi zinayi ya Davide, itapachikika pamenepo; mbendera yakale kwambiri padziko lapansi, nthawi yoyamba yomwe inawulutsidwa kwa zaka thuu sauzande.

⁵⁷ Yesu anati, “Pamene mkuyu udzaphukire masamba ake, m’badwo uno sudzadutsa.”

⁵⁸ Ndipo apa iwo anali akuwabweretsa okalamba amenewo mmenemo, ndipo anati, “Chiyani? Kodi mukubwera kudzafera mu dziko lakwanu?”

⁵⁹ Anati, “Ayi, ife tabwera kuti tidzamuwone Mesiya.”

60 Ndipo, m'bale, ine ndikukuuzani inu, ife tiri pa khomo! Ndi amenewo antchitowo, iwo amene akuyembekezera kumusi uko. Osati gulu ili la Ayuda omwe angakunyengeni inu ndi mano anu onyengezerawo ngati angathe, ameneyo si Myuda amene Iye akumukamba. Koma ndi iwo kumusi uko amene asunga— malamulo ndi zinthu, ndipo sankadziwa nkomwe kuti kunali Mesiya.

61 Ndipo M'bale...ku Stockholm, M'bale Petrus, anawatimizira iwo kumeneko Chipangano Chatsopano millioni, ndipo pamene analandira iwo anali akuwerenga iwo. Iwo anati, "Chabwino, ngati uyu ali Mesiya, tiloleni ife timuwone iye akuchita chizindikiro cha mneneri, ndipo ife timukhulupirira iye."

62 Ndi zogwirizana bwanji ndi utumiki wanga! Ndinali mkati mwa maora awiri a zipata za Yerusalemu, kuti ndikaloweko, ndipo ine ndinali ku Cairo, Egypt. Ndipo ndinali ndikuyenda kumeneko, ndipo Mzimu Woyera unati, "Usapite tsopano."

63 Ine ndinaganiza, "Ine ndimangolingalira. Tikiti yanga inali itagulidwa kale, ine ndiri panjira yanga. Munthuyo ali kunjya uko kuti akomane nane, gulu lonselo, masukulu ndi zina zotero."

64 Ine ndinayenda patsogolo pang'ono, ndipo Mzimu unati, "Usapite kumeneko! Iwe usapite kumeneko."

65 Ine ndinabwerera kwa wogulitsa matikiti, ine ndinati, "Ine ndikusintha tikiti iyi. Ine ndikufuna ndipite kumtunda ku Athens, Greece, ku Mars Hill.

66 Ndipo iye anati, "Chabwino, tikiti yanu ndi ya ku Yerusalemu, bwana."

67 Ine ndinati, "Ine ndikufuna kupita ku Athens m'malo mopita ku Yerusalemu." Mzimu Woyera ukuyembekezera, ora limenelo silinafike pakali pano. Izo si zoyenera basi.

68 Onani:

...anawasindikiza antchito a Mulungu wathu pamphumi pawo,

Akuti, Musavulaze dziko lapansi, ...mpaka ife... titasindikiza antchito a Mulungu wathu pamphumi pawo. (aliyense akudziwa kuti icho ndi Chisindikizo cha Mzimu Woyera; penyani)

Ndipo ndinamva chiwerengero cha iwo amene anasindikizidwa:...(tsopano, ngati iwo si Ayuda, penyani izi) ...ndipo pamenepo anasindikizidwa handiredede ndi forte-foro sauzande onse a mafuko a ana a Israeli. (osati Wamitundu mwa iwo. Apo ndi pa nthawi ya kumapeto)

69 Penyani! Fuko la Yuda, thwelofu sauzande; fuko la Rubeni, thwelofu sauzande; ndipo mpaka mmusi, Gadi, thwelofu

sauzande; Nefitali, ndi—ndi—ndi njira yonse mpaka kwa Aseri, ndi—ndi Zebuloni, ndi mafuko thwelofu sauzande onse awa a Israeli. Ndipo thwelofu kuchulukitsa thwelofu ndi chiyani? Handiredede ndi forte-oro sauzande. Alipo handiredi ndi forte-oro sauzande, Ayuda! Osati Amitundu, Ayuda! Icho si chinthu chochita ndi Mkwatibwi. Chotero a Mboni za Yehova amalakwitsa pa chiphunzitsa chawo. Baibulo limanena momveka bwino kuti iwo ndi “Ayuda,” ndipo osati Amitundu. Iwo ndi antchito a Mulungu, ndipo Wamitundu sankatengedwa konse ngati wantchito. Ndife ana aamuna ndi aakazi, osati antchito.

⁷⁰ Tsopano werengani zonse za Izo. Monga munthu akudya chivwembe, anati, “Izo ndi zabwino, koma tiloleni ife tikhale ndi zina za izo.” Chabwino, Mulungu ali ndi zochulukira za Izo apa. Tsopano, tangozindikirani. Tsopano, tsopano ife tiri pa ndime ya 8:

Ndi a fuko la Zebuloni... anasindikiza thwelofu sauzande. Fuko lonse la Yosefe anasindikizidwa thwelofu sauzande. A fuko la Benjamini anasindikizidwa thwelofu sauzande.

⁷¹ Mwaona, Yohane, pokhala Myuda, anawazindikira aliyense a iwo, anawona mafuko thwelofu a Israeli; thwelofu sauzande kuchokera mu fuko lirilonse, thwelofu kuchulukitsa thwelofu kukhala handiredi ndi forte-oro sauzande. Ndi awo pamenepo, osati Mpingo, Ayuda. Baibulo linanena apa, iwo onse anali “ana a Israeli,” fuko lirilonse linatchulidwa.

⁷² Tsopano penyani, ndime ya 9:

Zitatha izi (tsopano apa pakubwera Mkwatibwi)...

Zitatha izi ndinawona, ... taonani, khamu lalikulu, limene palibe munthu akanatha kuliwerenga, ...

⁷³ Ndi amenewo adindo anu a mkachisi, iwo ndi handiredede ndi forte-oro sauzande basi, malo aang’ono chabe, olondera mkachisi apang’ono chabe amene ati adzakhale ndi Mkwatibwi; Iye yekha—omuperekeza Iye basi. Ndiwo handiredede ndi forte-oro sauzande, ndi omuperekeza Mkwatibwi; adindo a m’kachisi.

⁷⁴ Penyani! Inde, ndikudziwa kuti mubwerera kuno ku ya 14, ndi kuti, “Bwanji, iwo ali ndi Mkwatibwi kulikonse kumene iwo...” Mwamtheradi! Adindo amayenda ndi mfumukazi kulikonse kumene iye akupita. Zoonadi! Koma kodi iwo anali chiyani? Iwo sanali kanthu koma operekeza, ndipo ndicho ndendende basi chimene Lemba limanena kuti izo ziri apa.

⁷⁵ Zindikirani:

Ndipo zitatha izi... ndipo, taonani, khamu lalikulu, limene palibe munthu akanakhoza kuliwerenga, mwa mafuko onse, ... abale, ... anthu, ndi lirime, ... (apo pali Mkwatibwi wanu wa Amitundu

akubwera, chabwino) . . .awa *anayima . . .pamaso pa Mwanawankhosa*, (apo pali Mpulumutsi wawo, Mwanawankhosa, osati lamulo; Mwanawankhosa, Chisomo) . . .*atavekedwa miinjiro yoyera, . . .*(penyani, mu maminiti pang'ono, muwone ngati miinjiro yoyera si chiyero cha woyera mtima) . . .*ndi kanjedza m'manja mwawo*;

Ndipo iwo anafuula ndi mawu aakulu, . . .(ngati ichi si chitsitsimutso cha Chipentekoste, ine sindinamvepo chimodzi) . . .*akuti, Chipulumutso kwa Mulungu wathu yemwe wakhala pa mpando wachifumu, ndi kwa Mwanawankhosa.*

Ndipo angelo onse anaimirira mozungulira mpandowachifumu, ndi pafupi ndi akulu ndi zamoyo zinayi, . . .anagwa pa a . . . pamaso pa mpando wachifumu pankhope zawo, ndipo analambira Mulungu,

Akunena, Amen: Dalitso, . . .ulemelero, . . .nzeru, . . . mathokozo, . . .ulemu, . . .nyonga, mphamvu, zikhale kwa Mulungu wathu ku nthawi za nthawi. Amen.

76 Izo zikumveka ngati nthawi ya msonkhano wamsasa, sichoncho izo? Izo zidzakhala! Ameneyo anali ndani? Handirede forte-foro sauzande? Ayi konse! Chiwerengero chachikulu ichi chimene palibe munthu . . .mwa mitundu yonse, malirime, ndi mafuko. Kodi iwe sukuwona, mzanga wokonedwa?

77 Tsopano penyani, mungowerenga Zimenezu. Tsopano:

Ndipo mmodzi wa akulu anayankha, anati kwa ine, Kodi awa ndi ndani ndi . . .amene avala miinjiro yoyera? ndipo iwo akuchokera kuti?

78 Mkuluyo anati kwa Yohane, amene anali Myuda amene anazindikira handirede ndi forte-foro sauzande, anati, “Tsopano, inu munawadziwa iwo, iwo onse ndi Ayuda. Koma awa ndi ndani? Iwo akuchokera kuti?” Mukuona zomwe wamkuluyo ananena? “Mmodzi wa akulu anayankha,” (amenewo ndi akuluakulu pa Mpandowachifumu) “anandiyankha ine, anati, ‘Kodi awa ndi ndani amene avala miinjiro yoyera ndi chiyani? Ndipo iwo akuchokera kuti? Tsopano, ife tonse tikuwadziwa Ayuda ndi pangano lawo ndi zina zotero, koma kodi awa anabwera liti?’” Tsopano penyani:

Ndipo ine ndinati kwa iye, Bwana, inu mukudziwa. (“Ine—ine—ine sindikutero,” Yohane anati, “izo zangondidutsa ine. Ine sindikudziwa.”) Ndipo iye anati kwa ine, Awa ndi iwo amene anatuluka mu zisautso zazikulu, (“Kudutsa mu mayesero ndi zowopsya zambiri izi, zovuta ndi misampha, ine ndabwera kale.” Mukuona?) . . .awa atuluka mu zisautso zazikulu, ndipo atsuka miinjiro yawo, . . .(mu mpingo? Kodi izo

zikumveka bwino?) . . . *atsuka miinjiro yawo, ndipo ayiyeretisa iyo mmagazi a Mwanawankhosa.*

. . . *iwo ali patsogolo pa mpandowachifumu wa Mulungu, ndipo amamutumikira Iye usana ndi usiku . . . (ndani amanditumikira ine kunyumba kwanga? Mkazi wanga. Nkulondola uko?) . . . ndi mu Kachisi Wake: . . . (ameneyo ndi amene amakhala ndi ine m'nyumba mwanga ndi chuma changa, ndi mkazi wanga. Iye ndi amene amakhala ndi ine, ndipo amachapa zovala zanga, ndipo amandikonzera zinthu zanga) . . . ndipo iye amene akhala pa mpando wachifumu adzakhala pakati pawo. (Oh, mai, mvetserani!)*

Ndipo *iwo sadzamvanso njala, . . . (zikuwoneka ngati iwo anali ataphonya zakudya zingapo pobwera kumeneko) . . . komanso iwo sadzamva ludzu kenanso; ngakhale dzuwa silidzawunikira pa iwo kenanso, ngakhale kutentha kulikonse.*

Pakuti Mwanawankhosa amene ali pakati pa mpandowachifumu adzawadyetsa iwo, ndipo adzawatsogolera iwo ku akasupe a madzi amoyo: ndipo Mulungu adzapukuta . . . misozi yonse m'maso mwawo. (ndi Ameneyo apo, ndi ameneyo Mkwatibwi wanu)

⁷⁹ Ndi amenewo handiredi ndi forte-foro sauzande anu, ndi amenewo antchito anu. Chotero “ana a Ufumu” apa, munthu wokonedwa amene anafunsa funsolo, ndi . . . amene anafunsa funso lodziwika bwino ili. Ine ndikuganiza kuti ndalisiya ilo kumbuyo kuno mu a . . . kwinakwake, koma “pamene iwo adzaponyedwa kunjja,” sizikutanthauza kuti iwo adzachotsedwa mmalingaliro a Mulungu. Iwo akuponyedwa kunjja kwa zopindula zauzimu za nyengoyo. Mwaona, kwa kanyengo pang’ono chabe.

⁸⁰ Chifukwa, pamene mneneri anawona Israeli mu tsiku ili limene iye ankabwerako, iye anati, “Chabwino, kodi Israeli adzakhhalapo pamene Sabata lidzachotsedwe, ndipo—ndipo iwo amagulitsa pa Sabata mofanana ndi tsiku lina lirilonse, ndi zinthu zonse izi?” Iye anati, “Chabwino, kodi Inu—kodi Inu mudza . . . Kodi Israeli adzaiwalidwa kwathunthu?”

⁸¹ Iye anati, “Kumwamba ndi kotalika bwanji? Kodi dziko lapansi ndi lakuya bwanji? Yezani izo ndi ndodo yomwe ili patsogolo panu.”

Iye anati, “Ine sindingakwanitse!”

⁸² Iye anati, “Ngakhalenso Ine sindingathe kuiwala Israeli nkomwe.” Ayi ndithu! Israeli sadzaiwalidwa.

⁸³ Chotero, inu mukuona, *nthawizonse* ndi *Muyaya* ndi zinthu ziwiri zosiyana. Israeli anaponyedwa kunjja, koma osati kuchoka

mmalingaliro a Mulungu. Ndipo Paulo akuziyankhula izo apa, ngati ine ndikanakhala ndi. . . ndikanakhala ndi nthawi yoti ndiwerenge, kuti ndikhoze mwamsanga kufika ku Lemba limene. . . Ine ndikhoza kuwalozera iwo kwa inu, mwaona, izo zikubwera mmalingaliro anga.

⁸⁴ Paulo akuyankhula kumeneko, ananena zimenezo kuti ife Amitundu tisamale, momwe tikuyendera ndi zomwe tikuchita. Mukuona? Chifukwa ngati Mulungu sanalekerere nthambi yoyamba, mwaona, ndipo ife pongokhala ongomezanitsidwa, mwaona, . . . Ndipo Israeli, amene anachititsidwa khungu kwa kanthawi, iye anatero. Kwa kanthawi chabe, Israeli anachititsidwa khungu. Uko nkulondola, koma chophimbacho chidzachotsedwa mmaso mwawo. Ndipo apo ndi pamene Wamitundu wotsiriza adzabadwira mu Ufumu wa Mulungu, ndiye chophimba chawo chidzachotsedwa pamaso a Israeli. Ndipo iwo adzati, “Uyu ndi Mesiya Amene ife tinkayembekezera kuti tidzamuwone.” Uko nkulondola, koma khomo la Amitundu latsekedwa (chombo cha—chatsekedwa), palibenso—palibenso chisomo chinatsalira kwa Amitundu pa nthawi imeneyo.

⁸⁵ Tsopano, ine ndikutenga nthawi yochulukira pa funso limodzi. Ndipo wina akuti, “Tsopano inu simufika kwa langa.” Chabwino, tifulumira ndi kuwona ngati sitingathe kufika kwa ilo.

⁸⁶ Chabwino, apa pali a—lalitali. Ndipo chidutswa chirichonse cha ilo chimene mkaziyo anafunsa kapena mwamunayo anafunsa, kapena aliyense amene ali, ndi cholondola.

53. Kodi si zoonza kuti Ambuye Yesu sanafere dziko lonse lapansi, kutanthauza kuti aliyense pa dziko lapansi, koma makamaka . . . (Tsopano, ine ndikhoza kufotokoza izo, koma iye, mwamunayo kapena mkaziyo, aliyense amene ali, zikuwoneka ngati zolembe za mkazi.) . . . koma makamaka kwa awa—kani kwa awa mmadera onse a dziko lapansi, amene Atate anamupatsa Iye? Awa amene maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, Mulungu anawadzozeratu ku Moyo Wamuyaya, atawasankha iwo molingana ndi kukondweretsedwa Kwake Komwe kwabwino?

⁸⁷ Mwamtheradi, uko nkulondola! Ndiko kulondola ndendende. Yesu anafera. . . osati basi. . . Iye analinga.

⁸⁸ Tiyeni tiwone, ine ndikukhulupirira a. . . Ine—Ine ndikukhulupirira iwo anawerenga. . . funso likubwera pa izi:

54. Lemba mosakayikira limatiuza ife kuti awa ndi amene sadzakhlapo—ndi iwo amene sadzapulumutsidwa. Choncho. . .

⁸⁹ Ndiko kulondola ndendende. Lemba limatiuza ife kuti pali anthu amene anadzozedweratu ndi Mulungu kuti adzaweruzidwe.

⁹⁰ Kodi mungakonde kuwerenga zimenezo, kuchitira kuti nthawizonse zisamakhale mmalingaliro anu? Chabwino, tiyeni titembenuzire tsopano ku Bukhu la—la Yuda, Yuda akuyankhula apa.

Yuda, wantchito wa Yesu Khristu, mchimwene wake wa Yakobo, kwa iwo amene ayeretsewa ndi Mulungu Atate, ndi kusungidwa mwa Yesu Khristu, ndi kuyitanidwa:

⁹¹ Mukuona amene iye akuwalemba Iwo? Osati ochimwa, osati utumiki wa uvangeli wokha, koma kwa oyeretsedwa ndi oyitanidwa. Mwaona, iwo amene ali kale mu Ufumu.

Chifundo kwa inu, ndi mtendere, ndi chikondi, zichulukitsidwe.

Okonedwa, . . . ine ndikupereka kulimbika konse kuti ndikulembeni inu za chipulumutsa cha wamba, chinali choyenera kwa ine kuti ndikulembeni inu, ndi kuti ndikulimbikitseni inu. . . inu moonamtima mulimbikire chikhulupiriro chimene chinaperekedwa kamodzi kwa oyera mtima.

Pakuti pali anthu ena anakwawira mkati mosadziwika, amene anadzodzedwera kale ku kutsutsidwa uku, . . . (motani?) . . . akusandutsa chisomo cha Mulungu wathu kukhala chilakolako chonyansa, . . .

⁹² Odzozedwa a kalekale! Osati kuti Mulungu anakhala pa mpandowachifumu, ndipo anati, “Ndimupulumutsa munthu uyu, ndimutaya munthu uyo.” Izo sizinali zimenezo! Mulungu anafa, ndipo pamene Yesu anafa, chitetezero chinadzadza dziko lapansi lonse kwa munthu aliyense. Koma Mulungu, mwa kudziwiratu. . . Osati kuti Iye adzatero. . . Iye sakufuna kuti aliyense awonongeke. Iye ankafuna kuti aliyense adzapulumutsidwe. Chimenecho chinali Chake—icho chinali cholinga Chake Chamuyaya. Koma ngati Iye anali Mulungu, Iye ankadziwa yemwe akanati adzapulumutsidwe ndi yemwe akanati asadzapulumutsidwe. Ngati Iye akanati asadziwe, ndiye kuti Iye sanali Mulungu wopandamalire. Chotero Baibulo limaphunzitsa zimenezo. Kuti ife tidzakhoze. . .

⁹³ Ngati ife tikanakhala ndi nthawi yoti titembenuzire apa mu Aroma, mutu wa 8, ndipo inu mukanakhoza kuziwerenga izo. Aroma, mutu wa 9, malo ena ambiri mu Baibulo. Aefeso, mutu wa 1. Ndipo inu mukhoza kuwona kuti kusankha kwa Mulungu, kuti iko kukhoze kuyima motsimikiza, Mulungu anapereka pangano mopanda mangawa. Iye anamutumiza Yesu kudzawafera iwo amene Iye anawadziwiratu. Mukuona?

⁹⁴ Osati kungoti, “Chabwino, inu mukuti Mulungu sakudziwa ngati iye ati adzapulumutsidwe kapena ayi?” Mulungu ankadziwa kuti inu mudzapulumutsidwa, kapena ngati inu

mukanadzatero kapena ayi, dziko lisanayambe konse, kapena Iye sanali Mulungu.

⁹⁵ Kodi mukudziwa chimene mawu akuti *infinite* amatanthauza? Yang'anani pa...muyang'ane mu dikishonare ndipo mupeze chimene mawu akuti *infinite* amatanthauza. Bwanji, Iye anadziwa utitiri uliwonse umene ukanati udzakhalepo pa dziko lapansi, ntchentche iliyonse, utitiri uliwonse, nyongolosi iliyonse. Iye anadziwa izo zisanakhale konse mu kupezeka, kapena Iye sanali Mulungu. Ndithudi, Iye anadziwa izo. Chabwino.

⁹⁶ Kenako, mmenemo, Mulungu sakanati—sakananena, “Ine ndidzakutenga *iwe*, ndi kukutumiza iwe ku gehena; ndipo Ine ndidzakutenga *iwe*, ndi kukutumiza iwe Kumwamba.” Mulungu ankafuna kuti awiri nonse mudzapite Kumwamba. Koma mwa kudziwiratu Iye anadziwa kuti mmodzi adzakhala wamanyazi, ndipo winayo akanadzakhala njonda ndi Mkristu. Mukuona? Chotero Iye ankayenera kumutumiza Yesu kuti adzafe, kuti adzamupulumutse munthu uja amene Iye anamudziwiratu kuti ankafuna kuti adzapulumutsidwe. Kodi mukuzimvetisa zimenezo?

Tsopano tayang'anani apa:

Malemba mosakaikitsa amatiuza ife kuti awa ndi amene sadzapulumutsidwa.

55. Chotero ngati chitetezero chinaphimba onse... mafuko onse a Adamu, ndipo ena anatayika chifukwa sanazipangitse kuti apezeke pa lonjezo, kapena kupereka, sakanatero... akanatha...mfulu...iye adza...adzakhala mphamvu yayikulu kuposa zolinga Zamuyaya ndi zolinga za Mulungu Wamphamvuzonse? Kodi izo zidzakhala...(Munthuyo tsopano, pa funso lachiwiri ili, akufunsa.) Kodi chifuniro cha payekha cha munthu sichingakhale mphamvu yayikulu kuposa madongosolo Amuyaya ndi cholinga cha Mulungu Wamphamvuzonse?

⁹⁷ Ayi, m'bale wanga kapena mlongo. Ndithudi ayi! Palibe chirichonse champhamvu kwambiri...Chifuniro cha munthu sichingafanane ndi—cholinga Chamuyaya cha chiweruzo cha Mulungu. Izo sizingakhale, mwaona.

⁹⁸ Tsopano, funso lanu loyamba linali lolondola. Funso lanu lachiwiri sizingatheke, mzanga. Chifukwa yang'anani, yang'anani momwe zinalembedwera apa, onani: “Kodi chifuniro cha payekha cha munthu sichingakhale champhamvu yayikulu kuposa madongosolo Amuyaya ndi cholinga cha Mulungu Wamphamvuzonse?” Bwanji, ndithudi ayi. Kodi zingatheke bwanji kuti chifuniro cha munthu chikhale champhamvu yayikulu bwanji kuposa cholinga cha Mulungu Wamphamvuzonse? Ndipo munthu mu chikhaliidwe chake chachithupi kuti achite chimene iye akufuna kuchita,

mwamphamvu kwambiri kuposa chimene Wamuyaya, Mulungu wangwiro akanati adzakhale? Ndithudi ayi! Izo sizingatheke, mwaona. Mulungu Wamuyaya, Amene cholinga chake ndi changwiro, inu munganene bwanji kuti a—munthu wachithupi kumusi kuno, ziribe kanthu momwe aliri wolungama (ndipo iye akhoza kukhala), zolinga zake sizingafanane mwa njira iliyonse ndi izi: a—cholinga cha Mulungu Wamuyaya ndi Wamphamvuzonse.

⁹⁹ [Mlongo akuyankhula kwa M’bale Branham—Mkonzi]. Inde. [“Ndine ndikupepesa. Ine ndimangofuna kuti ndifunse funso, ndipo—ndipo inu simunamvetsetse chimene ine ndikutanthauza pamenepe.”] Eya, chabwino, mlongo. [“Ine sindimakhulupirira zimenezo nkome, ine ndimatanthauza ‘Cholinga Chamuyaya cha Mulungu chikuposa chifuniro cha munthu.’”]

¹⁰⁰ Uko nkulondola. Oh, chabwino, ine—ine ndawerenga izo molakwika ndiye, mwaona. Chabwino. Inde, inu mukulondola ndendende pamenepe, mlongo. Sindimadziwa kuti ndi lanu—funso lanu. Chabwino. Koma, taonani, pamene ine ndinazipeza izi apa, mwaona, . . . Tsopano ndiroleni ine ndiwone, “Kuphimba mtundu wonse wa Adamu, ndipo ena anatayika chifukwa sanazipangitse kuti apezake okha—okha ndi zopereka zake, kodi chifuniro chodzisankhira cha munthu sichingakhale mphamvu yayikulu kuposa madongosolo Amuyaya ndi cholinga cha Mulungu Wamphamvuzonse?” Mwaona, ine—ine ndinamasulira maganizo anu molakwika pamenepe. Inde, cholinga Chamuyaya cha Mulungu Wamphamvuzonse. Chabwino, izo zikukhazikitsa izo.

¹⁰¹ Ine ndikuganiza aliyense akumvetsa zimenezo. Inu mukutero, kwezani mmwamba manja anu. Icho—icho ndi cholinga Chamuyaya cha Mulungu Wamphamvuzonse, ndithudi chingakhale chapamwamba kuposa—pamwamba patali kuposa zomwe munthu angachite.

Tsopano:

56. Sindimavetsa kuwala pa ubatizo wa mmadzi, mu mutu wa 28 wa . . . Ndime ya 19, ya Mateyu. Kodi izi zikutanthauza chiyani?

¹⁰² Chabwino, tsopano, mwinamwake sizinganditengere ine kupitirira miniti yokha. Ndipo tiyeni pakhale wina atsegule ndi ine ngati inu mungafune, ku Mateyu, mutu wa 28, ndi ndime ya 19. Ndipo ife tipeza, basi chimene munthuyo ali. . . . tvente-faivi. . . . Tsopano, Iwo akupangani inu wamphamvu ngati inu mungakhale nawo Iwo. Iwo ndi—Iwo ndi abwino, inu mwaona. Iwo si uvangeli, koma Iwo. . . .

¹⁰³ Tsopano ndife. . . . Tsopano apa ndi pamene anthu amayesera kunena, “Muli kutsutsana mu Baibulo.” Tsopano, ine ndikufuna winawake kuti atsegule ku. . . . ndi Mateyu 28:19. Kapena, ayi, ine ndikufuna winawake. . . . Mateyu 28:19. Ine ndikufuna winawake

atsegule ku Machitidwe 2:38. Inu muli ndi Baibulo lanu pamenepo, M'bale Neville?

¹⁰⁴ Ndipo ine ndikufuna inu mudziwerengere nokha tsopano. “Ndipo ine ndikuwonetsani inu kutsutsana kosamalitsa mu Baibulo. Ndipo chimene a—Baibulo...Anthu amati ‘Baibulo silimadzitsutsa Lokha,’ Ndikufuna kuti inu muganizirepo izi.”

¹⁰⁵ Ndipo izi zimapangitsa anamatetule kukhala a imvi. Koma Ilo—Ilo ndi lophweka. Tsopano ndiwerenga Mateyu 28:19, inu muzinditsatira ine. Ndipo ena a inu ndi Machitidwe 2:38, mukonzekere pamenepo. Ine ndiyambira mpaka ndime ya 18, uwu ndi mutu wotsekera wa Mateyu:

Ndipo Yesu anadza ndipo analankhula kwa ake ophu-... analankhula kwa iwo, akuti, Mphamvu zonse zapatsidwa kwa ine kumwamba ndi padziko lapansi. (mphamvu za Atate ziri kuti?)

¹⁰⁶ Ngati mphamvu zonse Kumwamba ndi padziko lapansi zinaperekedwa kwa Yesu, Mulungu analibe mphamvu ndiye, sichoncho Iye? Kapena kodi Iye anangonena nkhani? Kodi Iye ankasereula? Iye ankatanthauza Zimenezo! Kodi inu simukukhulupirira kuti Iye ankatanthauza Zimenezo? Chabwino, ngati mphamvu zonse zinaperekedwa kwa Iye, ndiye mphamvu za Mulungu ziri? Iye anali Mulungu! Ndizo ndendende. Ndicho chinthu chokhacho chimene chiripo kwa izo. Ndizo zonse zomwe zinalipo. Mwaona, Iye anali Mulungu; kapena mwina pali winawake wakhala pamenepo, anali ndi mphamvu ina, alibenso izo pano. Mukuona? Chotero simungathe—inu simungasokoneze Iwo. Tizipeza izo pa chinthu chomwecho apa. Chabwino:

... Mphamvu zonse kumwamba ndi padziko lapansi ndi... kumwamba ndi padziko lapansi.

Pitani inu chotero, ... mukaphunzitse mafuko onse, kuwabatiza iwo mu dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera:

Kuwaphunzitsa iwo kuti asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu: ... taonani, Ine ndiri ndi inu nthawizonse, ngakhale mpaka kumalekezere a dziko lapansi.

¹⁰⁷ Machitidwe 2:38, tsopano winawake awerenge. Dikirani miniti yokha. Machitidwe, mutu wa 2, ndime ya 38. Tsopano, mvetserani mwacheru kwenikweni tsopano, ndipo mungokhala oleza mtima, ndipo ife tiwona tsopano. Tsopano, awa ndi masiku teni kenako Yesu atawauza iwo tsopano, Mateyu 28:19, “Chifukwa chake pitani, mukaphunzitse mafuko onse, kuwabatiza iwo mu dzina la Atate, la Mwana, ndi la Mzimu Woyera.”

¹⁰⁸ Tsopano, Petro, patadutsa masiku teni. . . Iwo sanalalikire konse ulaliki wina. Iwo anapita mu chipinda chapamwamba cha Yerusalemu, ndipo anakadikirira kumeneko (kwa masiku teni) kuti Mzimu Woyera ubwere. Ndi angati akudziwa zimenezo? Pamalo awa. Apa pali Petro, Petro ali ndi makiyi aku Ufumu. Chabwino, tiwona chimene iye akuchita. Mateyu, kapena ine ndikutanthauza Machitidwe 2, tiyeni titenge ndime ya 36:

Chifukwa chake lolani nyumba yonse ya Israeli idziwe ndithudi, kuti Mulungu wamupanga Yesu yemweyu, amene inu. . . wopachikidwa, awiri onse Ambuye ndi Khristu.

“Awiri onse Ambuye ndi Khristu.” Nzosadabwitsa, mphamvu zonse mmiyamba ndi pa dziko lapansi zinapatsidwa kwa Iye.

Ndipo pamene iwo anamva ichi, analaswa mu mtima mwawo, ndipo anati kwa Petro ndi. . . atumwi enawo, Amuna ndi abale, tichite chiyani?

Petro anayankha. . . *Petro anati kwa iwo, Lapani, aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.*

¹⁰⁹ Tsopano, pali kutsutsana, Mateyu anati, “Mukabatize mu Dzina: Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” ndipo Petro anati mu Machitidwe 2:38, patapita masiku teni, “Lapani, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu.”

¹¹⁰ Kenako nthawi yotsatira imene kulapa kunakambidwa—kunakambidwa, kapena, ubatizo, mu Baibulo, ndi Machitidwe a—mutu wa 8, pamene Filipino anapita uko ndipo anakalalikira kwa. . . kwa—kwa Asamariya. Ndipo iwo analandira Mzimu Woyera, ndipo anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu.

¹¹¹ Nthawi yotsatira yomwe kunakambidwa, inali pamene Amitundu anawulandira Iwo, Machitidwe 10:49:

Ndipo pamene Petro. . . anayankhula mawu awa, taonani, Mzimu Woyera unagwa pa. . . iwo amene anawamva iwo.

Pakuti anawamva iwo akulankhula mu malirime, ndi kumukuza Mulungu. Kenako Petro anati,

Kodi munthu angaletse madzi, powona kuti awa. . . alandira Mzimu Woyera monga ife tinachitira pachiyambi?

Ndipo iye anawalamulira iwo kuti abatizidwe mu dzina la Ambuye Yesu Khristu.

¹¹² Tsopano ndiroleni ine ndikhale ndi chinachake apa, ndingokuwonetsani inu chinachake chaching’ono kuti inu musaiwale icho; ndipanga kuwonetsera kwakung’ono. Ine

ndiyika. . . Ndi ingati miba- . . . mitundu ya anthu imene ilipo padziko lapansi? Ilipo itatu: anthu a Hamu, Shemu, ndi Yafeti. Ndi angati akudziwa zimenezo? Ife timachokera kwa ana atatu a Nowa amenewo. Anthu a Hamu, anthu a Shemu. . . Anthu a Yafeti ndi a Anglo-Saxon, anthu a Shemu ndi. . . Mibadwo itatu, ndiyo: Myuda, Wamitundu, ndi theka Myuda ndi Wamitundu. Tsopano, zindikirani, pamene izo apo. . . ndipo *uyu* ndi Hamu. . . Shemu, Hamu, ndi Yafeti.

¹¹³ Tsopano, nthawi yoyamba imene ubatizo unayamba wayankhulidwapo, unayankhulidwa ndi Yohane M’batizi. Ndi angati amadziwa kuti izo ndi zoono? Chabwino, ine ndichiyika *ichi* cha apa, cha apa, Yohane M’batizi. Ndipo Yohane ankawabatiza anthu mu mtsinje wa Yordano, kuwalamula iwo kuti akuyenera kulapa ndi kukonzana ndi Mulungu, ndi kugulitsa katundu wawo, ndi kuwadyetsa osauka, ndipo asilikali kuti akhutitsidwe ndi ndalama zawo, ndi kukonzana ndi Mulungu. Ndi angati akudziwa zimenezo? Ndipo anawabatiza iwo mu mtsinje wa Yordano, osati kuwakonkha iwo, osati kuwatsanulira iwo, koma anawamiza iwo! Ngati inu simukuwakhulupirira Iwo, apa pali lexicon, mufufuze ngati iwo si *ubaptizo*, chimene chiri “kubatiza, kumiza, kuyikidwa pansu, kukwiriridwa.” Tsopano, nthawi yoyamba imene ubatizo unayamba wayankhulidwapo, kunali kumeneko.

¹¹⁴ Nthawi yachiwiri imene ubatizo unayamba wayankhulidwapo, Yesu analamulira iwo, Mateyu 28:19.

¹¹⁵ Nthawi yotsatira imene ubatizo unayankhulidwa, inali Machitidwe 2:38.

¹¹⁶ Nthawi yotsatira imene ubatizo unayankhulidwa, munali mu mutu wa 8 wa Machitidwe.

¹¹⁷ Nthawi yotsatira imene ubatizo unayankhulidwa, inali mu—mutu wa 10 wa Machitidwe.

¹¹⁸ Ndipo kenako ife tinabwera kuchokera ku nthawi imene Yesu ananena, apa, “Pitani inu chotero, kaphunzitseni mafuko onse, kuwabatiza iwo mu Dzina la Atate, ndi la Mwana, Mzimu Woyera.”

¹¹⁹ Tsopano tiyeni tiliwongole Lemba ili, choyamba. Ine ndinakuuzani inu kuti “palibe Lemba limodzi mu Baibulo limene lingatsutse limzake.” Ndikufuna inu mundibweretsere ine. Ine ndafunsa zimenezo kwa zaka twente-sikisi, ndipo sindinalipezebe. Palibe Lemba limene limatsu- . . . Ngati izo zimatsutsa Ilo, ndiye iyo ndi nkhani yolembedwa ndi munthu. Ayi, bwana, mulibe kutsutsana mu Baibulo!

¹²⁰ Tsopano izi inu munati, “Nanga bwanji *zimenezo*?”

¹²¹ Apa panayima Yesu akuti, “Chifukwa chake pitani, mukaphunzitse mafuko onse, kuwabatiza iwo mu Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera.”

122 Ndipo Petro akutembenuka mmbuyo momwe, ndipo anati, “Lapani, aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu.”

123 “Ndi kumeneko kutsutsana kwanu.” Zikuwoneka ngati izo. Tsopano, ngati inu mukuwerenga ndi malingaliro achithupi, ndipo osati mtima wotseguka, izo zikhala kutsutsana.

124 Koma ngati mungawerenge Iwo ndi malingaliro otseguka, “Mzimu Woyera unazibisa izi pamaso pa anzeru ndi aluntha,” Yesu ananena chomwecho, ndipo anamuthokoza Mulungu chifukwa cha izo, “ndipo waulula Izo kwa makanda omwe angaphunzire.” Ngati inu muli ndi malingaliro, ndipo osati malingaliro odzikonda, koma mtima wololera kuti muphunzire, Mzimu Woyera udzakuphunzitsani inu zinthu izi.

125 Tsopano ngati sizikufanana . . . Inu munati, “Inu mukudziwa bwanji kuti mukulondola?” Chabwino, izo zikufanana ndi Lemba lina lonse. Ngati inu simutero, inu muli ndi kutsutsana kotheratu apa.

126 Tsopano ine ndikufuna kuti ndikufunsemi inu funso. Uwu ndi mutu womaliza wa Mateyu. Ine ndilitenga ilo mu mawonekedwe aang’ono, kuti aliyense wa inu . . . ana azimvetse Izo.

127 Mwachitsanzo, ngati inu munawerenga nkhani yachikondi, ndipo kumbuyo kwake iyo nkuti, “Ndipo Mariya ndi Yohane anakhala mosangalala mpaka kalekale.” Chabwino, inu mukudabwa kuti Yohane ndi Mariya anali ndani amene anakhala mosangalala mpaka kalekale. Tsopano, ngati inu mukufuna kudziwa amene Yohane ndi Mariya ali, kulibwino inu mubwerere koyambirira kwa bukhulo ndi kukapeza yemwe Yohane ndi Mariya ali. Kenako mubwerere kuno ndi kudzafufuza yemwe Mariya anali, ndi banja limene iye anachokerako; ndi yemwe Yohane anali, ndi banja limene iye anachokerako, ndi chimene dzina lake linali, ndi momwe iwo anakwatirirana, ndi zonse za izo. Nkulondola uko?

128 Chabwino, ndicho chinthu chomwecho powerenga Baibulo apa. Pamene . . . Taonani, Yesu sanati, “Pitani mukawabatize anthu mu dzina la Atate, mu dzina la Mwana, mu dzina la Mzimu Woyera,” momwe anthu autatu amabatizira. Palibe Lemba la zimenezo mu Baibulo. Iye sananene konse, “Mu maina (m-a-i-n-a), maina” a Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.

129 Iye anati, “Mu (d-z-i-n-a) dzina,” limodzi. Tayang’anani pa Baibulo lanu pamenepo ndipo mufufuze ngati izo ziri zolondola, Mateyu 28, “Mu *Dzina*.”

130 Osati “mu dzina la Atate, mu dzina la Mwana, . . .” umo ndi momwe mlaliki wautatu amabatizira. “Mu dzina la Atate, mu dzina la Mwana, ndi mu dzina la Mzimu Woyera.” Izo mulibe nkomwe mu Baibulo.

131 “Kenako mu dzina . . .” Inu munati, “Chabwino, ndiye mu dzina la ‘Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.’” Ndiye kuti pali Dzina linalake pamenepo.

132 Chabwino, kodi *atate* ndi dzina? Ndi angati akudziwa kuti *atate* si dzina? *Atate* ndi udindo. *Mwana* si dzina. Ndi angati akudziwa kuti *mwana* si dzina? Ndi abambo angati ali muno? Kwezani dzanja lanu. Ndi ana angati ali muno? Kwezani manja anu. Chabwino, ndani wa inu dzina lake liri “Mwana”? Ndani wa inu dzina lake liri “Atate”? Chabwino, *Mzimu Woyera* si dzina, *Mzimu Woyera* ndi chimene Iwo uli. Ndi anthu angati ali muno? Kwezani dzanja lanu. Mukuona? Ndi zimenezotu, *Mzimu Woyera* ndi chimene Iwo uli. *Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera*, palibe lililonse la iwo limene liri maina; palibepo dzina kwa izo.

133 Chabwino, ndiye, ngati Iye anati, “Kabatizeni mu Dzina la Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera,” ife kulibwino tibwerere mmbuyo ndi kukafufuza Amene Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera ali. Tiyeni titembenukire mmbuyo ku mutu wa 1 wa Mateyu ndiye, tiwone Yemwe Munthu uyu anali amene ife tikuyenera kumabatiza mu Dzina liti. Ndipo ife tikuyamba tsopano ndi Mateyu, mutu wa 1, ndi ndime ya 18. Muwerenge mwatcheru, nonse.

134 Tsopano, inu amene munafunsa funsoli, ine ndikufuna kuti ndipereke kuwonetsera pang’ono apa. Tsopano ndiyika zinthu zitatu apa kuti inu mumvetse bwino, (ndipange kuwonetsera) Mabaibulo awa ndi mabukhu, kuti ndipange kuwonetsera.

135 Chabwino, ine ndikufuna inu mundiyang’ane ine mwatcheru, ndipo aliyense anditsatire ine tsopano. Tsopano, *uyu* apa ndi Mulungu Atate. *Uyu* apa ndi Mulungu Mwana. *Uyu* apa ndi Mulungu Mzimu Woyera. Tsopano, ndi angati akumvetsa? Inu munene monditsatira ine. Uyu ndi ndani pansi *apa*? [Osonkhana akuti, “Mzimu Woyera.”—Mkonzi]. Mzimu Woyera. Uyu ndi ndani ali *apayu*? [“Atate.”] Uyu ndi ndani *apa*? [“Mwana.”] Tsopano, umo ndi momwe autatu amakhulupirira zimenezo, Mwaona, izo zimatipanga ife kukhala achikunja, aawisi basi monga izo zingakhoze kukhalira.

136 Myuda; ndicho chifukwa chake inu simungachite kanthu ndi Myuda. Iye anati, “Inu simungamuduledule Mulungu mu zidutswa zitatu ndi kumpereka Iye kwa Myuda.” Koma, ndithudi ayi, inu simunganditerenso ine. Mukuona? Ayi, bwana. Iye ndi Mulungu mmodzi. Ndizo ndendende. Osati Milungu itatu. Tsopano zindikirani momwe—momwe—momwe Izo ziriri zophweka.

137 Tsopano ife tifufuza. Tsopano, ndani ali . . . *Uyu* ndi Ndani? Wina ayankhule tsopano. Mulungu Mwana. Nkulondola uko? *Uyu* ndi Mwana. Chabwino, ndiye Atate Ake ndi Mulungu. Nkulondola uko? Ndi angati akukhulupirira kuti Atate Ake ndi Mulungu? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Ndi angati

akukhulupirira kuti Mulungu ndi Atate wa Yesu Khristu? Chabwino.

Tsopano kubadwa kwa Yesu Khristu kunali motere: . . .

¹³⁸ Tsopano ife tikubwerera kuti tipeze Amene Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera ali, amene Mateyu anati “kabatizeni mu Dzina la.” Mwaona, Dzina; osati maina tsopano, chifukwa iwo sangakhale maina, chifukwa palibepo dzina pamenepo.

Tsopano kubadwa kwa Yesu Khristu kunali motere: Pamene . . . amayi ake Mariya anapalidwa ubwenzi ndi Yosefe, iwo asanakumane pamodzi, iye anapezeka ali ndi mwana wa Mulungu Atate. (Kodi Baibulo limanena zimenezo? Kodi Baibulo limati chiyani?) . . . iye anapezeka ali ndi mwana wa Mzimu Woyera.

¹³⁹ Ndiye ndi uti mwa awa ali Atate Ake? Tsopano, Baibulo linanena kuti *uyu* ndi Atate Ake, ndipo Yesu ananena kuti *uyu* anali Atate Ake. Tsopano, ndi Mmodzi uti amene ali Atate Ake? Tsopano, ngati Iye anali ndi atate awiri, tsopano nanga bwanji izo? Ngati Iye anali ndi atate awiri, Iye ndi mwana wapathengo.

¹⁴⁰ Tsopano tiyeni tingowerenga mopitirira pang’ono:

Kenako Yosefe mwamuna wake, pokhala munthu wolungama, sankafuna kumunyazitsa iye kugulu, koma aningalira kuti amusiye iye mwamseri.

Koma pamene iye ankasinkhasinkha pa zinthu izi, taonani, mngelo wa Ambuye anawonekera kwa iye mu loto, akuti, Yosefe, iwe mwana wa Davide, usawope kudzitengera kwa iwe Mariya mkazi wako: pakuti icho chimene chikuyembekezeredwa mwa iye ndi cha . . . [Osonkhana akuti, “Mzimu Woyera”—Mkonzi].

¹⁴¹ *Chiyani?* Mzimu Woyera? Chabwino, zingatheke bwanji kuti Atate akhale Atate Ake, ndi Mzimu Woyera kukhala Atate Ake nthawi yomweyo? Tsopano, Iye anali ndi atate awiri ndiye, ngati uko kuli kulondola. Ayi, bwana! Mzimu Woyera NDI MULUNGU. Mzimu Woyera NDI MULUNGU. Chotero Mulungu ndi Mzimu Woyera ndi Munthu yemwe yemweyo, kapena Iye anali ndi atate awiri.

¹⁴² Mwaona, ife tipeza yemwe Yohane ndi Mariya anali, pakapita kanthawi. Chabwino, ife tipeza ngati Petro ndi Mateyu ankayesera kuti azitsutsana wina ndi mzake kapena ayi, tiwona ngati Lemba limadzitsutsa Lokha. Ndi kusowa kwa kumvetsa kwauzimu. Uko nkulondola.

Koma pamene anali kusinkhasinkha pa izi. . .

¹⁴³ Ine ndapapeza pamenepo, ndime ya 20. Tsoapano ya 21:

Ndipo adzabala mwana wamwamuna, . . . (Munthu yu, anali a ndani awa? Munthu Mmodzi, Mulungu.) . . .

ndipo iwe udzamutcha dzina lake... (Chiyani?) [Osonkhana akuyankha, "YESU"—Mkonzi]. . . pakuti Iye adzapulumutsa anthu ake ku machimo awo.

. . . izi zonse zinachitidwa, kuti . . . chikakwaniritsidwe chimene chinanenedwa ndi Ambuye mwa mneneri, kuti,

Taonani, namwali adzakhala ndi pakati, ndipo adzabala mwana wamwamuna, ndipo adzamutcha dzina Lake Emanuele, . . . mwa kutanthauzira, Mulungu ali nafe.

144 Ndiye kodi Yohane ndi Mariya anali ndani amene anakhala mosangalala mpaka kalekale? Anali ndani Amene anati, "Chifukwa chake pitani, mukaphunzitse mafuko onse, kuwabatiza iwo mu dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera"? Kodi Atate anali ndani? Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera? [Winawake akuti, "Yesu."—Mkonzi]. Ndithudi, Ilo linali. Zedi, palibe kutsutsana kwa izo. Osati pang'ono. Izo zimangowongola Lembu. Iye anali Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Mulungu anali (Emanuele) akukhala ndi ife, akukhala mu thupi lotchedwa "Yesu."

145 Tsopano, chiphunzitso chaumodzi cha mpingo wa Umodzi, ine ndithudi sindimagwirizana nacho, kuganiza kuti Yesu ndi mmodzi monga chala chanu chiri chimodzi. Iye ankayenera kukhala ndi bambo. Ngati Iye sakanatero, Iye akanakhala bwanji atate Ake Omwe? Ndipo ngati Atate Ake anali munthu monga wa Utatu amanenera, ndiye kuti Iye anabadwa mwapathengo ndi atate awiri. Chotero, inu mwaona, inu nonse mukulakwitsa potsutsana. Mukuona?

146 Koma Choonadi cha izo ndi, kuti awiri onse Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, ndi Umunthu umodzi. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. . . okhala mu kachisi wa thupi, kuti achotse tchimo mu dziko lapansi. Ndiko kulondola ndendende, "Mulungu nafe." Tsopano, chotero, pamene Mateyu 28:19 . . .

147 Tsopano, inu mufufuze Malemba, ndipo pamene inu mungapeze pamene munthu mmodzi mu Baibulo . . . (Tsopano taganizani za zimenezo, tsopano musalole kuti izi zikudutseni inu.) . . . pamene munthu mmodzi mu Baibulo anayamba wabatizidwapo mu dzina la "Atate," ndi "Mwana," ndi "Mzimu Woyera," mudzabwerere kwa ine ndi kudzandiuza ine kuti ndine wachinyengo, ndipo ine ndidzayika chikwangwani pa nsana wanga ndi kudzayenda kudutsa mu mzinda. Izo mulibemo mu Malemba, kuchokera ku Genesis mpaka Chivumbulutso. Koma munthu aliyense mu Baibulo amabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu!

148 Inu mukuti, "Dikirani miniti, mlaliki. Nanga bwanji Yohane? Iye sanabatize mu dzina lirilonse!"

149 Chabwino, ife tifufuze chimene chinachitika; tiyeni titembenuzire ku—ku ku—Machitidwe, mutu wa 19. Pamenepo ndi pamene ife timapeza ophunzira a Yohane. Munthu aliyense anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, kupitirira mpaka tsopano ife tikupeza gulu ili cha apa. Machitidwe, mutu wa 19. Ndipo tiyeni tiyambe kuwerenga tsopano, ndipo ife tikupeza ophunzira a Yohane:

Ndipo zinachitika, . . . pamene Apollo (yemwe anali woyimira milandu, wotembenuka) anali ku Korinto, Paulo atadutsa magombe akumtunda kwa . . . Efeso: iye anawapeza ophunzira ena, (iwo anali otsatira a Yesu)

150 Ngati inu munangozindikira mutu wapambuyo tisanafike pamenepo, iwo anali ndi nthawi yopambana chomwecho mpaka iwo ankafuula ndi kusangalala. Ndi angati akudziwa kuti izo nzoona? Ndipo Aquila ndi Priscilla anali pa msonkhanowo. Ndipo Paulo ndi Sila anamenyedwa ndi kukwapulidwa, ndipo anayikidwa mu ndende. Nkulondola uko? Ndipo iwo anabwera cha kuno, ndipo anamupeza Aquila ndi Priscilla. Ndipo iwo anali ali ndi chitsitsimutso kumtunda uko ndi mlaliki wa Baptisti, dzina lake Apollo, amene ankatsimikizira mwa Malemba kuti “Yesu anali Khristu.” Tsopano Paulo anamupeza iye:

. . . Paulo atadutsa magombe akumtunda kwa . . . Efeso: . . . anapeza ophunzira ena,

Iye anati kwa iwo, Kodi inu munalandira Mzimu Woyera kuyambira pamene inu munakhulupirira? . . .

151 Tsopano, iwe mzanga wokonedwa wa Baptisti, ngati izo sizikugogoda—zothandizira kuchokera pansi pa zaumulungu zanu, pamene iwe unati “unalandira Mzimu Woyera pamene iwe unakhulupirira.”

152 Koma Paulo ankafuna kuwafunsa Abaptisti awa, “Kodi inu munalandira Mzimu Woyera chikhulupirireni?” Tsopano penyani zomwe iwo ananena:

. . . Ndipo iwo anati kwa iye, Ife tikudziwa . . . ngati kuli Mzimu Woyera uliwonse.

Ndipo iye anati kwa iwo, Ku chiyani . . . (tsopano, ngati inu mukufuna kupeza lexicon ya Chigriki apa, iyo ikusonyezani inu, “Inu munabatizidwa motani?”) . . . Ku chiyani . . . momwe inu munabatizidwira? Ndipo iwo anati kwa iye, Pansi pa Yohane kumbuyo kuno. Yohane anatibatiza ife.

153 Tsopano ndikufuna kuti ndikufunsi: Ngati inu mukanakhala ndi ubatizo umenewo, kodi inu mukanakhutitsidwa nawo? Munthu yemweyo amene anayenda ndi Yesu kupita mu mtsinje, nadipo anamubatiza Yesu Khristu, munthu yemweyo anawabatiza anthu awa. Umenewo ndi ubatizo wabwino kwambiri: osati kukonkha, osati kuthira,

koma kumizidwa mu Yordani wakale wamatope pa malo omwewo amene Yesu anabatizidwa. Taganizani za zimenezo.

154 Paulo anati, “Kodi inu munalandira Mzimu Woyera chikhulupirireni?” Iwo... iye...

Iwo anati, “Ife tikudziwa...kaya pali Mzimu Woyera uliwonse.”

Iye anati, “Inu munabatizidwa motani?”

Iwo anati, “Ife tinabatizidwa.”

“Inu munabatizidwa bwanji?”

“Kwa Yohane!”

155 Tsopano penyani chimene Paulo ananena. Onani apa:

Ndipo iye anati kwa iwo, . . . kodi inu munaba- . . . Kwa Yohane . . . Ndipo iwo . . .

Ndipo kenako Paulo anati, Yohane ndithudi ankabatiza . . . ubat- . . . ku kulapa, akunena kwa . . . anthu, . . . iwo akuyenera kukhulupirira pa iye amene anadza pambuyo pake, uko ndikuti, pa Yesu Khristu.

156 Mwaona, Yohane ankangobatiza ku kulapa, koma ubatizo wa madzi mu Dzina la Yesu ndi wa chikhululukiro cha machimo. Chitetezero chinali chisanapangidwe pamenepo, machimo sakanakhoza kuchotsedwa. Tsopano . . . Uko kunali kungoyankha kwa chikumbumtima, monga pansu pa lamulo. Luka 16:16 akuti, “Chilamulo ndi aneneri zinalipo mpaka kwa Yohane, kuyambira pamenepo Ufumu ukulalikidwa.” Tsopano penyani. Ndipo . . . Penyani.

Ndipo Paulo anati a- . . . (tsopano penyani) . . . Kodi inu munalandira . . .

157 Ya 5—ndime ya 5:

Ndipo pamene iwo anamva ichi, iwo anabatizidwa (kachiwiri) mu dzina la . . . Yesu Khristu.

158 Kulondola uko? Ndiye anthu awa, anthu mu Machitidwe 2, anabatizidwa mu Dzina la Yesu. Ayuda anabatizidwa mu Dzina la Yesu. Amitundu anabatizidwa mu Dzina la Yesu. Ndipo munthu aliyense mu Baibulo lonse amabatizidwa mu Dzina la Yesu.

159 Tsopano mupeze malo amodzi amene wina aliyense anayamba wabatizidwapo mwanjira ina iliyonse, ndipo ine ndidzabwerera komwe kuno ndi kudzakuwonetsani pamene mpingo wa Katolika umavomereza izo, ndi kudzanena kuti inu mugwadire kwa izo. Ndipo anati, “Pakhoza kukhala pali Achiprotestanti ena opulumutsidwa chifukwa ali ndi ziphunzitsa zochepe za Chikatolika, monga ubatizo mu dzina la ‘Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera’; kuti mpingo woyera wa Katolika uli ndi ufulu wosintha mwambowo kuchoka ku Dzina la Yesu, kukhala ‘Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,’

ndipo mpingo wa Chiprotestanti umavomereza zimenezo.” Uwu sumatero, ine ndimakhala ndi Baibulo. Ine ndimakhulupirira Baibulo.

¹⁶⁰ Inu mukuti, “M’bale Branham, kodi inu mumawalamulira anthu kuti abatizidwenso?” Mwamtheradi! Paulo anatero, apa.

¹⁶¹ Tsopano penyani, tiyeni titenge Agalatiya 1:8, ndi kupeza chimene Paulo ananena:

...ngakhale ife, kapena mngelo wochokera kumwamba, akalalikira uthenga wina uliwonse kwa inu. . . mulole iye akhale wotembereredwa.

¹⁶² Ndi zimenezotu, “Ngati ife kapena mngelo.” Ndipo Paulo, munthu yemweyo, anawalamulira anthu kuti abatizidwenso kachiwiri amene anali ndi ubatizo wabwinoko kuposa umene inu mwakhala nawo, m’bale wanga; chifukwa Yohane M’batizi anali msuweni Kumene wa Yesu, msuweni wachiwiri; akumubatiza msuweni wake yemwe mu mtsinje wa Yordano, ndipo anapotoloka ndi kukawabatiza ophunzira a Yohane. Ndipo Yesu anati, “Izo sizingagwire ntchito!” kapena Paulo ananena Izo, ndipo anawalamulira iwo kuti abatizidwenso kachiwiri mu Dzina la Yesu Khristu iwo asanalandire Mzimu Woyera; atatha kufuula ndi kumutamanda Mulungu ndi kukhala ndi nthawi yopambana, kukhala ndi chachikulu—chitsitsimutso chachikulu, ndi kutsimikizira mwa Baibulo (ndi zaumulungu zawo) kuti Yesu anali Khristu. Ndi angati akudziwa kuti ilo ndi Lemba? Mutu wa 18. Ndithudi ilo liri. Ndi zimenezotu. Chotero palibe funso kwa Ilo.

¹⁶³ Tsopano ndiroleni ine ndikupatseni mfundo yofunikira yaing’ono. Tsopano, iye sanachoke mu dongosolo, koma mu Luka. . . Mateyu, mutu wa 16. Yesu, pamene iwo ankatsika pa phiri, Iye anati, “Kodi munthu amati Ine Mwana wa munthu ndine yani?”

¹⁶⁴ “Ena amati Inu ndi ‘Eliya,’ ndipo ena amati Inu ndi ‘aneneri,’ ndipo ena amati Inu ndi ‘ichi, icho.’”

¹⁶⁵ Iye anati, “Koma inu mukuti Ndani?”

¹⁶⁶ Petro anati, “Inu ndi Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo.”

¹⁶⁷ Penyani! “Wodala ndiwe, Simoni Bar-yona (mwana wa Yonasi), thupi ndi magazi sizinawululire konse Izi kwa iwe.” Amen!

¹⁶⁸ Mwaona, Izo zikuyenera kubwera mwa vumbulutso lauzimu. Thupi ndi mwazi sizinamuuze konse Abele kuti iye ankalakwitsa (Kaini, kuti iye amalakwitsa), sizinamuuze konse Abele kuti “Kaini akulakwitsa.” Koma Ilo linali vumbulutso limene Abele anali nalo, “Anali magazi!” Tikubwera ku funso limenelo mu mphindi pang’ono. Anali magazi, osati zipatso, amene anatichotsa ife mmunda wa Edeni. “Anali magazi,” ndipo Abele, mwa vumbulutso lauzimu, zinawululidwa ndi Mulungu

kuti anali magazi, ndipo iye, “Mwa chikhulupiro,” Ahebri 11:1 amati, “anapereka kwa Mulungu nsembe yoposa ya Kaini. Chimene, Mulungu analandira nsembe yake.” Ndi zimenezotu. Mwaona, iye anapereka iyo mwa chikhulupiro, mwa vumbulutso.

¹⁶⁹ Tsopano penyani, “Thupi ndi mwazi sizinawulule izi kwa iwe,” (kudutsa mpaka kwa Ambuye Yesu) “koma Atate Anga amene ali Kumwamba awulula Izi kwa iwe. Ndipo pa thanthwe ili (vumbulutso la Yesu Khristu) . . . Pa thanthwe ili Ine ndidzamazungu Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizingakhoze kuwulaka Iwo.” Izo ndi zimene Iye ananena. Lauzimu vumbu- . . . “Ndipo Ine ndikuti iwe ndi Petro, ndipo Ine ndidzakupatsa iwe mafungulo a Ufumu. Ndipo chirichonse . . . Chifukwa iwe uli ndi mpita wotseguka wauzimu pakati pa kuno ndi Kumwamba. Thupi ndi mwazi: iwe sunatenge konse seminare, iwe sunatenge konse kuphunzira, iwe sunatenge konse a—a—maphunziro aza fioloje. Koma iwe unadalira pa Mulungu, ndipo Mulungu anaulula Izo kwa iwe, ndipo ndi mwamtheradi Malemba omveka amene akumangiriza Izo pamodzi. Ine ndikuti ndiwe Petro, uko nkulondola, ndipo Ine ndikupatsa iwe mafungulo; ndipo chimene uchimanga pa dziko lapansi, Ine ndidzachimanga Kumwamba; chimene iwe udzamasula pa dziko lapansi, Ine ndidzachimasula icho Kumwamba.”

¹⁷⁰ Ndipo Petro anali wolankhulira pa Tsiku la Pentekoste, pamene iwo onse ankachita mantha kuti ayankhule, iye anayankhula ndipo anati, “Inu amuna aku Yudeya ndi inu amene mukukhala mu Yerusalemu, mulole ichi chidziwike kwa inu ndipo mvetserani ku Mawu anga. Iwo sanaledzere monga inu mukuganizira, powona kuti ndi ora lachitatu la tsiku, koma ichi ndi chimene chinanenedwa ndi mneneri Yoweli. ‘Zidzachitika mmasiku otsiriza,’ atero Mulungu, ‘Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa mnofu wonse. Ana anu aamuna ndi aakazi adzanenera. Ndipo pa mdzakazi Wanga, wantchito, Ine ndidzatsanulira za Mzimu Wanga. Ndipo Ine ndidzawonetsera zizindikiro mmiyamba mmwamba ndi pa dziko lapansi, ndi mizati ya utsi ndi nthunzi. Izo zidzachitika lisanadze Tsiku lalikulu ndi lowopsya la Ambuye, kuti aliyense amene adzaitana pa Dzina la Ambuye adzapulumutsidwa.’” Ndi zimenezotu. Oh, mai.

¹⁷¹ “Ndiroleni ine ndilankhule momasuka kwa inu za mbadwa yakale Davide,” iye anati, “iye anafa ndipo anayikidwa mmanda, ndipo manda ake ali ndi ife mpaka lero. Chotero, pokhala mneneri, iye anawona . . . anamuwona Iye padzanja Lake lamanja, ‘Ndipo Ine sindidzasunthidwa. Ndiponso thupi Langa lidzakhala mu chiyembekezo chifukwa Iye sadzasiya moyo Wanga mu gehena, ndiponso sadzalola Woyera Wanu Uyo kuti awone chivundi.’”

¹⁷² “Ndipo Davide anafa,” iye anati, “ndipo anayikidwa

mmanda, ndipo manda ake ali ndi ife lero. Koma pokhala mneneri, iye anawoneratu kudza kwa Mmodzi Wolungamayo, Amene Mulungu anamupanga zonse ziwiri Ambuye ndi Khristu.” Oh, mai. Amenewo ndi Malemba anu. Ndi icho chinthucho. Ndi chimenecho.

¹⁷³ Tsopano ife tikupeza apa, ndiye, kuti njira yolondola, ndipo njira yeniyeni, ndi njira yokhayo yomwe inayamba yadzozedwapo. . . Ndipo Petro anali ndi mafungulo, ndipo pa tsiku limene iye analalikira, iwo anati. . . Tsopano penyani, apa pali Mpingo woyamba. Inu Akatolika mvetserani kwa Izi. Inu a Campbell mvetserani kwa Izi. Inu Abaptisti ndi Amethodisti mvetserani kwa Izi. Ndipo inu Achipentekoste mvetserani kwa Izi. Church of God, Anazarene, Pilgrim Holiness, mvetserani kwa Izi.

¹⁷⁴ Petro anali ndi mafungulo, ndipo iye anali ndi ulamuliro, kapena Yesu ananama. Ndipo nkosatheka kuti Iye aname, “zinthu ziwiri zosasinthika, ndi zosatheka kuti Mulungu aname.” Iye anali ndi mafungulo. Yesu anamupatsa iye mafungulowo. Pamene Iye anawuka pa—pa tsiku lachitatu monga choncho, Iye anali ndi mafungulo a imfa ndi, gehena, koma osati mafungulo aku Ufumu. Petro anali nawo! Ndizo kulondola ndendende.

¹⁷⁵ Ndipo tsopano penyani, Petro, iwe uli ndi mafungulo akulendewera pa mbali yako, ndipo iwe ukulalikira. Funso likubwera, otembenuka mtima oyamba a mpingo watsopano. Mpingo Wachikhristu woyambirira. Tsopano Akatolika, tsopano Abaptisti, Amethodisti, Apresbateria, kodi inu muli pa chiphunzitso cha Mpingo Watsopano? Fufuzani ngati inu muli.

. . . Mwamuna *ndi abale, ife tingachite chiyani?*

. . . *Petro* anaimirira ndipo *anati. . . Lapani, . . . aliyense wa inu. . .* (yang’ana pamenepo, mnyamata; momwe iwe ukuikira mafungulo awo apa, Khristu adzawayika iwo Kumwamba) . . . *Lapani*, aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe *mu dzina la Yesu Khristu. . .* (Umo ndi momwe mumalowera mu Izi) . . . *ku chikhululukiro cha machimo* anu, *ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.*

¹⁷⁶ Mafungulowo anamveka “kiliki” apa, ndipo iwo anapita “kiliki” Apo. Ndi chifukwa chake ophunzira a Yohane ankayenera kubwera ndi kudzabatizidwanso, kachiwiri, mu Dzina la Yesu Khristu (iwo asanapite Kumwamba), kukalandira Mzimu Woyera. Iye anasunga Mawu Ake. Chotero izo sizikukusokonezani inu tsopano, sichoncho izo? Mukuona? Ndithudi, Mateyu 28:19 anali maudindo, osati Dzina.

¹⁷⁷ Chabwino, kodi ife tiri ndi nthawi yochuluka bwanji? Kodi ife tingakhale ndi maminiti fifitini owonjezera kuti tiyankhe mafunso ena angapo mofulumira kwenikweni? Kodi tingatero?

Chabwino, ife tifulumira mwachangu. Ine ndiri ndi awiri apa pansu, ine ndimafuna kuti ndifulumire, kujowinana ndi izi, ngati ine ndingathe. Kenako ine ndikhoza kudzawatenga ena onsewo Lamlungu mmawa.

57. Kodi Kaini anali mphukira ya serpenti? (Ili ndi labwino.) Ngati ndi choncho, nchifukwa chiyani Eva sanatenge pakati mpaka Adamu atamudziwa iye?

Momwemonso . . . Funso lotsatira liri momwemonso:

58. Kodi unali a—mtengo weniweni umene Eva anadyamo chipatso? Iye anawona kuti chinali chabwino kudya.

¹⁷⁸ Chabwino, m'bale, mlongo, aliyense amene anali, tiyeni tibwerere mu Genesis ndipo tikapezemo chinachake apa. Tiyeni tipite ku Genesis 3:8, ngati inu mungafune. Chabwino, ndipo mumvetsera mwatcheru kwenikweni tsopano.

¹⁷⁹ Tsopano ndiyibweretsa nkhaniyo. Izo zonse zinali zangwiro ndi zoyera, panalibe tchimo kapena chodetsedwa. Tsopano ine nditenga . . . lanu . . . funso loyamba ili poyamba. Mtengo mmoyo . . . pakati pa munda, pakati pa mtengo. *Mtengowo* unali “mkaziyo.” Tsopano ine nditsimikizira izo kwa inu mwa Malemba ngati mutangokhala opirira maminiti pang’ono.

¹⁸⁰ Ife titenga poyamba ngati iye anali . . . ngati iye anatenga pakati asanamudziwe Adamu kapena ayi, kapena pambuyo . . . Mvetserani:

Ndipo iwo anamva liwu la AMBUYE Mulungu akuyenda mmunda, ndipo mu kuzizira kwa tsiku: ndipo Adamu ndi mkazi wake anadzibisa okha pamaso pa AMBUYE Mulungu pakati pa mitengo ya m'munda.

Ndipo AMBUYE . . . anamuyitana Adamu, ndipo anati . . . Iwe uli kuti?

Ndipo iye anati, ndinamva liwu lanu mmunda, ndipo ine ndinawopa, chifukwa ndinali wamaliseche; . . . (tsopano, iye samadziwa kuti dzulo lake; chinachake chinali chitachitika, chinachake chinamuululira iye kuti anali maliseche) ndipo ndinadzibisa ndekha.

Ndipo iye anati, Ndani wakuuza iwe kuti uli wamaliseche? Kodi iwe wadya za mtengowo, . . . ?

¹⁸¹ Kudwa za mtengowo kunamupangitsa iye kuzindikira kuti anali maliseche? Monga ine ndimanenera nthawi zambiri, (iyi si nthabwala, sindikutanthauza izo ngati nthabwala) “Koma ngati kudya maapulo kunapangitsa akazi kuzindikira kuti ndi amaliseche, kulibwino tiperekenso maapulowo.” Mukuona? Iwo sunali umaliseche. Iwo sunali mtengo, apulo amene iwo anadya, izo zinali zogonana. Penyani:

. . . Kodi iwe wadya za mtengo, umene ine ndinakulamulira iwe kuti usadye?

Ndipo mwamunayo anati, Mkazi amene inu mwandipatsa ine, kuti akhale ndi ine, iye anandipatsa ine. . . mtengowo, ndipo ine ndinadya.

Ndipo AMBUYE. . . anati kwa mkaziyo, Ichi ndi chiyani chimene iwe wachita? Ndipo mkaziyo anati, Serpenti anandinyenga ine, . . . (huh?) . . . Serpenti anandinyenga ine, ndipo ine ndinadya. (nthawi yayitali iye asanakhale ndi pakati, mwaona, ndi Adamu)

¹⁸² Adamu anamudziwa iye, ndipo iye anatenga pakati ndipo anabala—ndipo anabala Abele.

¹⁸³ Koma ndikufuna kuti ndikufunsemi inu, basi kuchokera ku kamvedwe kenikeni. Tsopano kuti nditsimikizire kwa inu kuti iye anali mtengo, mkazi aliyense ndi mtengo wa chipatso. Ndi angati amadziwa zimenezo? Kodi inu sindinu chipatso cha amayi anu? Ndithudi, inu muli. “Ndipo pakati pa chipatsocho, kapena pakati pa mtengowo, chipatso chimene iye sankayenera kuchikhudza.”

¹⁸⁴ Ngati inu mungazindikire, kodi Yesu sanali Mtengo wa Moyo? Kodi Iye sanalonjeze mu Mateyu Woyera, kapena, Yohane Woyera, mutu wa 6, “Ine ndine Mkate wa Moyo umene umachokera kwa Mulungu Kumwamba”?

¹⁸⁵ Ngati mwamuna adya za mkazi. . . Ndipo taonani, kupyolera mu kubadwa kwa. . . mwa mkazi, ife tonse timafa; chifukwa ndife oti tizifa (nkulondola uko?) kupyolera mu kubadwa kwa mkazi. Kupyolera mu kubadwa kwa mwamuna, ife tonse timakhala ndi moyo wosatha. Mkazi ndi mtengo wa imfa, mwamuna ndi mtengo wa moyo; pakuti mkazi alibe ngakhale moyo mwa iye. Ndizo kulondola ndendende. A—nyongolosi ya moyo imatuluka kuchokera mwa mwamuna, molondola. Imakalowa mwa mkazi, ndipo mkaziyo si kanthu koma chofungatira; ndipo mwanayo samalumikizidwa, ndi mchombo wokha. Palibe chidutswa chimodzi cha magazi a amayi omwe amakhala mwa khandalo; wobadwa mu magazi ake, koma sipamakhala chidutswa chimodzi *mwa* mwanayo. Pitani mukafuze. . . kapena mukawerenge bukhu la dokotala, kapena mukafunse dokotala wanu, inu mudzawona. Iwo mulibe mmenemo, ayi, bwana, palibe chidutswa chimodzi cha iwo nkomwe. Iye ndi dzira chabe, ndizo zonse. Ndipo moyo umachokera kwa mwamuna.

¹⁸⁶ Umenewo ndi mtundu wokongola wosonyeza kuti kudzera mwa mkazi, kudzera mu kubadwa kwachibadwa, ife tonse tikuyenera kufa, chifukwa ndife akufa kuyamba ndi kuyamba; ndipo kokha kudzera mwa Mwamuna Khristu Yesu tikhoza kukhala ndi moyo. Ndipo apo pali mitengo iwiri mmunda wa Edeni. Kodi inu simukuiwona imeneyo?

¹⁸⁷ Ndipo penyani! Ndipo mu tsiku limenelo panali Mkerubi anaikidwa kuti azilondera mtengo uwu. Kutu ngati iwo adzalawe

konse Mtengo wa Moyo umenewo, iwo onse akanadzakhala moyo kwanthawizonse. Ndi angati akudziwa zimenezo? Iwo onse adzakhala ndi moyo kosatha. Ndipo nthawi yoyamba iwo akanalawa iwo...Mngelo anati, "Ife tizilondera Iwo." Ndipo anayika Akerubi pamenepo ndi malupanga amoto aja cholozza kummawa kuti azilondera Iwo. Iwo anawutengera Iwo kubwerera Kummawa, ndipo ankalondera Mtengo umenewo ndi malupanga amoto kuchitira kuti iwo asakhoze kulowamo kuti awutenge Iwo (Mtengo uwu).

¹⁸⁸ Ndipo pamene Yesu anabwera, Iye anati, "Ine ndine Mkate wa Moyo, kuti munthu akadya Mkate uwu sadzafa konse." Ndi umenewo Mtengo wanu.

¹⁸⁹ Ndi uyo mkazi wanu, apo pali kugonana kwanu komwe kumabweretsa imfa. Motsimikiza basi monga pali chikhumbo chogonana, ilipo imfa yosiyidwa ndi icho. Ndipo motsimikiza basi monga kulipo kubadwa kwauzimu, ulipo Moyo Wamuyaya wosiyidwa ndi Iwo. Imfa imabwera kudzera mu kubadwa kwa mkazi, ndipo Moyo umabwera kudzera mu kubadwa kwa Mwamuna. Amen! Ndi zimenezotu.

¹⁹⁰ Tsopano tiyeni tibwerere kwa Kaini. Kodi inu mungandiuze ine kumene mzimu umenewo ndi kuyipa mtima kumeneko kunachokera? Ngati Kaini...penyani, ngati Kaini anali mwana wa Adamu yemwe anali mwana wa Mulungu, kodi choyipa chimenecho chinachokera kuti? Chinthu choyamba pamene iye anabadwa, iye ali ndi udani, iye anali wakupha, iye anali wa nsanje. Ndipo tsopano tengani chikhalidwe cha abambo ake, chiyambi kumene pachiyambi, Lusifara, ndipo iye anali pachiyambi...iye ankamuchitira nsanje Mikaeli, chimene chinayambitsa vuto lonselo. Ndi angati akudziwa zimenezo? Ndipo Kaini anali chikhalidwe cha atate wake, chimene iye anamuchitira nsanje m'bale wake ndipo anamupha iye. Changwiro chimenecho...chirengedwe chimenecho sichikanatuluka mu mtsempha wangwiro umenewo. Icho chinabwera...chinkayenera kutulukira mu mtsempha wopotozedwa uwu. Ndipo zindikirani Kaini, mwamsanga pamene iye anabadwa.

¹⁹¹ Ndipo kenako Abele anabadwa pambuyo pake, kenako iye anakhala ndi pakati mwa Adamu, ndipo iye anamdziwa—anamudziwa iye ndipo anabala mwana wamwamuna Abele. Ndipo Abele anali choyimira cha Khristu; ndipo pamene—pamene Abele anaphedwa, Seti anadzatenga malo ake; imfa, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro cha Khristu, mwa choyimira.

¹⁹² Koma, tsopano, Kaini ankapembedza; ntchito zake zonse zachithupi, chimodzimodzi monga mpingo wachithupi lero: iwo amapita ku tchalitchi, iwo amapembedza. Kaini ankapembedza; iye sanali wachikunja, iye sanali wachikominisi. Kaini anali wokhulupirira; iye ankapita kwa Mulungu, iye anamanga guwa.

Iye anachita chinthu chirichonse chachipembedzo chimene Abele anachita, koma iye analibe vumbulutso lauzimu la chifuniro cha Mulungu. Lidalitsike Dzina la Ambuye! Ndi zimenezotu. Kodi inu mukuziwona Izo? Iye analibe vumbulutso lauzimu, ndipo ndiro liri vuto ndi mpingo lero. Ndipo Yesu anati Iye akanadzamanga Mpingo Wake pa vumbulutso lauzimu limenelo. Inu mukumvetsa Izo? Oh, mai, maso anu akhoza kutseguka tsopano. Mwaona, vumbulutso lauzimu.

¹⁹³ Kaini anabwera: iye anamanga guwa, iye ankapembedza, iye anabweretsa nsembe, iye ankagwada pansu, iye ankatamanda Mulungu, iye ankapembedza Mulungu, iye ankachita chirichonse chachipembedzo chimene Abele anachita. Ndipo Mulungu anamukana iye kotheratu chifukwa iye analibe vumbulutso lauzimu!

¹⁹⁴ Tsatirani mzere womwewo uwo wa Kaini: chotsika mmusi mpaka ku chombo, kuchokera mu chombo mpaka kukalowa mu Israeli, kuchokera ku Israeli kupita kwa Yesu, ndipo kuchokera kwa Yesu mpaka lero; ndi kuwona ngati mpingo wachithupi umenewo, wachikhazikitso, wowuma ndi wokhuthala, wa usikolala, ndikutanthauza amuna amene ali ndi Malemba, amene amadziwa chiphunzitso chonse ndi zafiolole, iwo akhoza kufotokoza izo, mnyamata, basi monga *choncho*, koma popanda vumbulutso lauzimu! [M'bale Branham anakhwachitsa zala zake—Mkonzi]. Uko nkulondola. Chimenecho ndi chiphunzitso cha Kaini.

¹⁹⁵ Baibulo linati, “Tsoka kwa iwo! chifukwa iwo anapita mu chiphunzitso cha Kaini, anathamangira mu zolakwa za Balaamu, ndipo anawonongeka mu kalankhulidwe kokopa ka Korah.” Bukhu lomwelo, Yuda, iye anati, “Iwo anakonzedweratu ku chiweruzo ichi.” Ndithudi, iwo ali. Mukuona? Kodi Balamu anali chiyani? Iye anali bishopu. Iye anali woyang'anira mpingo. Iye anabwera pamenepo mwachikhazikitso basi monga iye akanakhalira. Iye anapereka. . . Tayang'anani pa iye atayima pamwamba apo mwa otchuka, atayima pamenepo mu kutchuka kwawo kwakukulu. Ndipo iwo sanali achikunja, iwo anali okhulupirira.

¹⁹⁶ Limenelo—fuko limenelo la Mowabu linatuluka mwa mwana wamkazi wa Loti. Loti amene ankakhala. . . mwana wamkazi wa Loti amene anakhala ndi atate wake, ndipo anatenga pakati, ndipo anabala mwana, ndipo mwanayo anali. . . anaphukitsa fuko la Moabu. Ndipo iwo anali chipembedzo chachikulu. Anthu aakulu, amaluma, ndipo iwo anali ndi akalonga ndi mafumu ndi otchuka. Iwo anali ndi mabishopu ndi makadinolo ndi chirichonse.

¹⁹⁷ Ndipo apa pakubwera gulu la oyera odzigudubuza, gulu lina, Israeli; gulu laling'ono lachikulire limene linali lopanda chipembedzo, azipembedzo zosiyanasiyana. Ndipo iwo anachita

chirichonse chimene chinalipo pa mapu choti chichitidwe, choipa nachonso. Koma chimene icho chinali, iwo anali ndi vumbulutso lauzimu, ndipo Mulungu anali ndi iwo mu Lawi la Moto.

¹⁹⁸ Oh, ine—ine ndikudziwa iwo anali ndi zinthu zachithupi, ndipo anthu anati, “Gulu lotero la obwerera mmbuyo monga choncho, palibe choti nkuchita koma kuwathamangitsira iwo kunja.” Koma iwo anali ndi vumbulutso lauzimu, ndipo iwo anali ndi Thanthwe lokanthidwa, iwo anali ndi njoka yamkuwa, iwo anali ndi Lawi la Moto likupita limodzi ndi iwo. Aleluya! Ine ndikudziwa inu—inu mukuganiza kuti ndine wokondwa, koma ine sindiri. Ine ndikungomverera bwino.

¹⁹⁹ Zindikirani! Pamene ndinaganiza, “Mulungu yemweyo, lero, amakhala ndi ife.” Ilo likadali vumbulutso lauzimu la Mawu. Ndithudi, ilo liri. Ndi zolondola Kwamuyaya. Lidalitsike Dzina la Ambuye! Inde, bwana.

²⁰⁰ Apa panayima iye pamenepo, wachikhazikitso; gulu lija la Abaptisti ndi Apresbateria anayima pamwamba pa phirilo, ndipo anamutengera bishopu wawo kumeneko. Ndipo iwo anali achipembedzo basi, ndipo mtundu womwewo wa chipembedzo, iwo ankapembedza Mulungu yemweyo. Iwo anati, “Yang’anani panso apo pa mulu wa zinyalala uwo. Bwanji, iwo alibe nkomwe chipembedzo. Iwo si kanthu koma gulu la osokosa, okuwa, oyera odzigudubuza.”

²⁰¹ Nkulondola uko? Ndendende, iwo anali. Ngati inu simukukhulupirira kuti iwo anali oyera odzigudubuza, bwererani mu Genesis ndi kukapeza pamene iwo anawolokera. Ndipo chozizwitsa chinachitidwa, ndipo Miriamu anatenga nkhotcho ndipo anapita kumusi ku gombe, akuwomba iyo; akuvina mu Mzimu, ndipo Mose anayimba mu Mzimu. Ngati ilo si gulu la zomwe ife timadzitcha omasuka. . . oyera odzigudubuza, sindikudziwa chomwe icho chiri; akuyimba ndi kulumphu ndi kumamtamanda. Ndipo nthawi zonse mafuko ankawada iwo, koma Mulungu anali nawo. Iwo anali ndi vumbulutso lauzimu, ankatsatira Lawi la Moto lija.

²⁰² Ndipo Moabu anati, “Tsopano, tayang’anani kuno. Ife tiwaitana makadinolo onse ndi mabishopu onse, ndi akulu onse, ndipo tiwatengera iwo kunja kuno. Ife tichita chinachake pa izo, chifukwa ndife fuko lachipembedzo. Ife sitilola kuti zosokoneza zimenezo zisakanikirane mu chipembedzo chathu chabwino.”

²⁰³ Ndipo kotero iwo anawatengera iwo kunja uko. Ndipo iwo anamanga maguwa thwelofu; ndizo ndendende basi zomwe Israeli anali nazo, maguwa thwelofu. Iwo anayikapo nsembe thwelofu pa iwo, ng’ombe; ndendende basi zomwe Israeli anali nazo, zomwe Mulungu ankafuna. Iwo anayika nkhusa thwelofu pa iwo, kuimira kudza kwa Ambuye Yesu Khristu; nkhusa thwelofu mmalo onsewo.

204 Anthu onse otchuka, mabishopu ndi onse, anayima mozungulira. Iwo ankayatsa nsembe. Iwo anapemphera, iwo anakweza manja awo kwa Yehova ndipo anati, “Yehova, timvereni ife!” Kodi iwo ankayesera kuchita chiyani? Ndipo Balaamu wawo wakale anapita monga choncho, ndipo Mzimu unatsikira pa iye. Ndithudi (koma iye anali wachithupi).

205 Mzimu ukhoza kugwera pa wachinyengo, Baibulo linatero. Inu munandimva ine ndikuphunzitsa izo, tsopano. “Mvula imagwera pa olungama ndi osalungama.” Koma izo zikuyenera kufanizidwa ndi Mawu, apo ndi pamene inu mumazipeza izo.

206 Ndiye pamene iye anatero, ndipo a...pamene Mzimu, ngakhale, unali pa iye unanena Choonadi, iye anayesera kutemberera Israeli, ndipo anadalitsa Israeli.

207 Tsopano, ngati Mulungu amangolemekeza mpingo wabwino, ndi bishopu wabwino, ndi m’busa wodabwitsa, gulu la anthu ophunzira, Iye anali wokakamizika kuti avomereze nsembe imeneyo, chifukwa iye anali wolondola mwachikhazikitso basi monga Israeli anali wolondola; koma iye analibe vumbulutso lauzimu la Mawu ndi chifuniro cha Mulungu. Ndi zimenezotu, ndiko kusiyana kwake lero.

208 Tamuwonani Yesu. Iwo anati, “Kutali ndi munthu ameneyo. Ife tikudziwa kuti iye ndi Msamariya. Iye ndi wopenga. Kodi iwe ungatiphunzitse ife? Chabwino, iwe unabadwa mu chigololo. Iwe sunali kanthu koma mwana wapathengo woti ubwere naye. Abambo ako ndi ndani? Ukuti Mulungu ndi abambo ako, wonyoza iwe! Bwanji, iwe ukutanthauza kutiyoza ife? Ife takhala tiri alaliki, ife takhala bishopu; kudzera mwa agogo-a agogo-a agogo-a agogo-a agogo athu aamuna anali alaliki ndi bishopu. Ife tinabadwa ndi kuleredwa mu mpingo. Ife tadutsa m’maseminare apamwamba kwambiri. Ife timawadziwa Mawu aliwonse mpaka ku chilembo. Ndipo iwe ukuyesera kuti utiphunzitse ife? Kodi iwe unapita kusukulu yake iti? Kodi maphunzira awa unawatenga kuti?”

209 Iye anati, “Ndinu wa...atate wanu mdierekezi,” anatero Yesu.

210 Iwo analibe zizindikiro ndi zodabwitsa pakati pawo. Iwo analibe machiritso Auzimu ndi zinthu pakati pawo. Iwo analibe madalitso pakati pawo. Koma Yesu anali mwamtheradi vumbulutso lauzimu la Malemba.

211 Iwo anati, “Bwanji, izo zinalembedwa *zakuti-ndi-zakuti*.”

212 Ndipo Yesu anati, “Inde, ndipo kwalembedwanso.” Koma Mulungu anamutsimikizira munthu Wake ndi zizindikiro zake.

213 Petro ananena chomwecho, pa Machitidwe 2, iye anati, “Inu amuna a Israeli; Yesu wa ku Nazarete, Mwamuna wotsimikizidwa ndi Mulungu mwa inu, ndi zizindikiro ndi zozizwitsa zimene Mulungu anazichita mwa Iye pakati, ndi

zimene inu nonse mukuzidziwa.” (ndi inu pamenepo) “Iye pokhala wopulumutsidwa ndi...ndi kudzi-...ndi Bungwe lalikulu la Sanhedrin kumtunda uko. Koma mwa kudziwiratu kwa Mulungu, Mulungu anamudzozeratu Iye kuti adzafe ndi imfa iyi. Inu mwamupereka Iye ndi manja ankhanza ndi oyipa. Inu mwamupachika Kalonga wa Moyo, Amene Mulungu wamuwukitsa. Ndipo ndife mboni zake.”

²¹⁴ Psyii, ndi mlaliki bwanji! Sanatero... iye sankatha ngakhale kulemba dzina lake lomwe, koma iye ankamudziwa Mulungu. Iwo anati iwo “anamvetsera kwa iye kuti iye anakhala ndi Yesu.” Ndithudi, ndi vumbulutso lauzimu. Oh, mai. Tsopano, ndi zimenezotu pamenepo.

²¹⁵ Kaini anali basi mu mzere umenewo, mpingo wachithupi umenewo uli mu mzere womwewo lero. Mpingo Wauzimu ukadali ndi Lawi la Moto, ukanali ndi zizindikiro, zodabwitsa, ukanali ndi Khristu yemweyo; chimene chikutsimikizira njira yonse kuchokera kwa mwanawankhosa wakufa, ndi mmunda wa Edeni, mpaka Kudza kwachiwiri kwa Mwanawankhosa. Mwamtheradi, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

²¹⁶ Ndipo mzere uja wa Kaini, achipembedzo ndi opukutidwa ndi ophunzira, kumatsika mmusi chimodzimodzi; mofanana basi, tsiku lirilonse mofanana basi. Otsutsa ndi ozunza, monga Kaini anali wa Abele, momwemonso iwo ali lero, ndipo akhala alipo ndipo adzakhalapo nthawizonse; achithupithupi, osakhulupirira. Uko nkulondola.

²¹⁷ Tsopano Genesis 3:8, ndiponso ine ndinayika 20 apa, ine ndimayang’ana kanthawi kapitako:

Ndipo Adamu anamutcha...Ndipo Adamu anamutcha mkazi wake...Eva; chifukwa iye anali mayi wa amoyo onse. (mwaona, izo zinachitika chinyengo ichi chitachitika kale)

²¹⁸ Kaini anali... “Tsopano dikirani!” Inu mukuti, “Zingatheke bwanji njoka, serpenti?”

²¹⁹ Koma, m’bale, penyani apa, Baibulo silimanena kuti iye anali serpenti; Baibulo linati, “Iye anali wothyathyalika kwambiri mwa zilombo zonse za mmundamo.” Iye sanali chokwawa, iye anali chilombo. Iye anali a...Ndipo kumeneko...

²²⁰ Ndipo ndiroleni ine ndingokupatsani inu ichi ngati chizindikiro chaching’ono pakati pathu, ngati inu mungathe. Pamenepo ndi pamene sayansi imasakanizika. Chinthu chapafupi kwambiri chimene iwo angachipeze kwa munthu, ndi chimpanzi. Ndi angati akudziwa zimenezo? Koma pali chinachake pakati pamenepo. Iwo sangapangitse mafupa a chimpanzi kukumana ndi mafupa a munthu, komabe ndi chinthu chapafupi kwambiri. Iwo akhoza kumubweretsa iye kuchokera kwa nanchidwe. Iwo akhoza kumubweretsa iye

kuchokera kwa mbululu. Iwo akhoza kumubweretsa iye mpaka kwa nyama ndi nyama iliyonse. Iwo akhoza kumubweretsa iye kukhala chimbalangondo. Inu mutenge chimbalangondo ndi kusendapo chikopa pa icho, icho chimangokhala ngati mkazi wamng'ono. Chinthu chomwe chomwecho basi. Mutengereni iye mmbuyo ndi chirichonse, kawaimitseni iwo pamene, ndi kupitako uko ndi kukamuchotsapo mkaziyo monga... kukamuimitsa mkaziyo monga choncho. Ndi chimodzimidzi basi monga ngati a—ngati a—ngati chimbalangondo. Phazi limayenda chimodzimidzi, ndipo dzanja limayenda monga chonchi, chimodzimidzi basi monga munthu. Koma chimpanzi chimayandikira kuposa pamene. Icho chimakhala pafupifupi, koma iwo sangachipeze icho.

²²¹ Apa pali chinsinsi chaching'ono, ngati inu mukufuna kuchidziwa icho. Inu mukudziwa pamene icho chiri? Izo zinabisika kwa iwo. Iwo akhoza kukumba mafupa onse amene iwo akuwafuna. Iwo akhoza kukumba... Osema akhoza kukumba, ndi sayansi, ndi a—ndipo wodziwa nthawi akhoza kuyeza masikelo a nthawi ndi miyeso ya atomiki, koma sadzazipeza izo. Pakuti ameneyo anali serpenti amene anali wofanana mochuluka ndi munthu kuposa china chirichonse chimene chinalipo padziko lapansi, ndipo Mulungu anamutemberera iye ndipo anamuyika iye pa mimba yake, ndipo iye anasandulika kukhala njoka popanda kufanana ndi munthu. Tsopano mungokanda mutu wanu, asayansi amenewo, ndipo muwalole iwo atenge izo kwa kanthawi.

²²² Koma Baibulo limanena kuti, “Iye anali wotheathathalika kwambiri mwa zilombo zonse za mmundamo.” Uko nkulondola. Iye anali cholumikizira chimenecho chimene chimayima pakati pa munthu ndi nyani, ndipo Mulungu anamutemberera iye ndipo anamuyika iye mmbuyo momwe pa mimba yake chifukwa cha—cha chinthu chimene iye anachita. Iye anamunyenga mkazi yuyu, ndipo iye anabala mwana wake wamwamuna woyamba amene anali Kaini, motsatira chikhalidwe kumene cha kudzoza kwa serpenti, mdierekezi, chimene chinadzalowa mwa serpenti, amene anachita zimenezo.

²²³ Ndipo kenako iye anakhala ndi pakati ndipo anabala, iye anakhala ndi pakati kachiwiri atatha kunyengedwa. Tsopano penyani, iye ananyengedwa, iye anali pafupifupi... Chabwino, iye analakwitsa. Koma iye, kwenikweni, anali wovomerezeka pamene iye anatenga pakati ndi mwamuna wake, pakuti izo zikanakhoza kukhala zambiri, nthawi zambiri mtsogolo, miyezi yambiri ndi masiku ambiri mtsogolo mwake; inu simungathe kudziwa zimenezo, ife sitikudziwa, koma iye anabala Adamu.

²²⁴ Ndipo wina anapeza funso, anati, “Chabwino, mwana... iye anati iye ankati... Pamene Kaini anabadwa, iye anati ‘ndalandira mwana wa Ambuye.’” Mwamtheradi, ndithudi, izo zinkayenera kutero. Ilo linali lamulo la chirengedwe. Ndizo

ndendende basi momwe inu muliri lero. Pamene inu mubadwa, Mulungu samangobwera pansi ndi kukupangani inu. Ndinu mphukira ya abambo ndi amayi anu. Ndipo inu mudzakhala a...kudzakhala a...ana anu adzakhala mphukira za inu. Ndiko kubalana nthawi zonse, mpaka mmusi, monga mitengo ya mbewu ndi zinthu monga choncho; koma kubwerera ku chiyambi. Ine ndikuyembekeza izo zikufotokoza izo.

²²⁵ Kodi tiri ndi nthawi yochuluka bwanji? Tiribenso iliyonse yowonjezera. Mvetserani kwa lina labwino ili kwa lotsatira... limene tidzalitenge Lamlungu: “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi...” (Ife tikufuna kudziwa zimenezo.) “...Khristu.” Panthawiyo... Tsopano, ine ndikuganiza nditenga Malemba ena, Malemba abwino pa izo [M’bale Branham akuyankha ili mu Gawo II, funso 60—Mkonzi.].

²²⁶ Apa pali labwino, basi monga...Kodi mungandilole ine miniti imodzi yokha kapena awiri, kuti ndiyankhe ili? Ilo likhoza kudziyankha lokha.

59. Pamene—pamene inu mukamati “oyipa sadzapsya kwa Muyaya,”... (Chabwino, tsopano ndiri ndi a Mboni za Yehova akuthawa, sichoncho ine?)... Pamene inu mukamati oyipa sadzapsya Kwamuyaya, kodi mumatanthauza mu gehena kapena mu nyanja ya moto? Ine ndikudziwa amanena mu Chivumbulutso (uwo ndi mutu wa 20) kuti gehena idzaponyedwa mu nyanja ya moto. Ngati iwo sadzapsya Kwamuyaya, ndiye chidzachitike ndi chiyani kwa iwo?

²²⁷ Basi monga ine ndangomaliza kumene kunena, m’bale kapena mlongo, aliyense yemwe anali; iwo adzatheratu, sipadzakhalanso kalikonse kwa iwo. Iwo anali ndi chiyambi, ndipo apo iwo athera; iwo sali kanthunso basi. Zidzakhala bwanji...iwo adzayaka motalika bwanji, izo ndizovuta kunena. Koma, penyani, apo...

²²⁸ Ngati inu mungakhoze kungotenga izi mmalingaliro anu, mwaona, ndi zophweka kwambiri. Pali mtundu umodzi wa Moyo Wamuyaya, ndipo umenewo umabwera kudzera mwa Mulungu Mwiniwake. Ndipo Mulungu yekha ndi Moyo Wamuyaya. Ngati inu mungangofika apa mu lexicon, mudzayang’ane liwu la Chigriki *Zoe*. *Zoe* ndi “Moyo Wamuyaya.” *Moyo Wamuyaya* ndi “Mulungu.” Ndipo Yesu anati, “Ine ndikupereka kwa iwo Moyo Wamuyaya.” Ndipo ngati mungayang’ane apa pa lexicon, ilo linati, “*Zoe*.” Umenewo ndi Moyo Wamuyaya wokhawo umene ulipo. Palibe malo mu Baibulo pamene Ilo limati kudzakhala gehena Wamuyaya, ilo linati iwo adzapsya “kwanthawi zonse.”

²²⁹ Tsopano, kuti mupeze mawu akuti *kwanthawizonse*, muyang’ane pa, *aeon*. Kodi inu munazindikira *apa*, mu Baibulo? Ndi angati anayamba amvapo izo zikunenedwa, “Ndipo ma aeons ndi ae-...”? Ndi angati akudziwa kuti *aeon* ndi “danga

la nthawi”? Bwanji, ndithudi, aliynse amadziwa kuti *aeon* ndi “danga la nthawi.”

²³⁰ “Ndipo iwo adzapsya moto kwa ma *aeon*,” ndiyo danga la nthawi. “Adzaponyedwa mu nyanja ya moto, ndipo adzawotchedwa kwa ma *aeon*.” *Aeons* amatanthauza “danga la nthawi.” Iwo akhoza kudzawotchedwa kwa zaka handirede milioni mu chilango koma, potsiriza, iwo adzayenera kufika kumapeto; kuti atheretu, pamodzi. Mwaona, chifukwa chirichonse chimene sichiri changwiwo ndi chopotozedwa kuchokera ku Changwiwo; ndipo icho chinali ndi chiyambi, chotero icho chikuyenera kukhala ndi mathero.

²³¹ Koma ife amene timakhulupirira mwa Ambuye Yesu Khristu tiri ndi *Zoe*, “Moyo Womwe wa Mulungu” mwa ife, ndipo tiri nawo Moyo Wamuyaya. Osati kukhala ndi moyo kwa nthawi za nthawi, wochimwa ali ndi moyo kwa nthawi za nthawi, koma ife tiri ndi “Moyo Wamuyaya.”

²³² M’bale Cox, osati kale litali, anali atakhala pa njira yanga ife tisanayike a...ife titayika miyala pamenepo, ndipo iye anatenga kakang’ono, kachidutswa kakale, ndipo anati, “M’bale Branham, iko kali ndi zaka zingati?”

²³³ “Oh,” Ine ndinati, “motsatira nthawi, inu mukhoza kunena kuti iko kali ndi zaka teni sauzande. Mtundu wina wa chaching’ono, chilombo chakale cha m’nyanja chomwe chinakhalapo nthawi ina, nyama yaying’ono ya m’nyanja, mwina inakhala mmbuyo mu mibadwo yapitayo.”

²³⁴ Iye anati, “Tangoganizani mmene moyo wa munthu uliri waufupi ku moyo *umene*wo.”

²³⁵ Ine ndinati, “Oh, koma, m’bale, chinthu chimenecho chiri ndi mathero, koma Moyo umene ife tiri nawo mwa Khristu ulibe mathero. Icho chikhoza kukhala moyo *nthawizonse* ziwiri kapena zitatatu, koma sichidzakhala ndi Moyo Wamuyaya konse, chifukwa Moyo Wamuyaya umachokera kwa Mulungu yekha.”

²³⁶ Wamuyaya, “Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya ndipo SADZATI adzabwere konse ku chiweruzo koma wadutsa kuchoka ku imfa wapita ku Moyo.” Ndi zimenezotu, inu mumapeza Moyo Wamuyaya pokhala wokhulupirira. Wosakhulupirira amakhala ndi moyo wa nthawizonse. Wamuyaya...wokhulupirira amakhala ndi Moyo Wamuyaya, ndipo sangawonongeke chifukwa Iwo ndi Wamuyaya.

²³⁷ Koma wokhulupirira, iye adzapita...Wosakhulupirira adzadutsa mdziko, iye adzakhala ndi zowawa, matsoka; chimene iye amachitcha kukhala ndi nthawi yayikulu, “whoopee, kukhala ndi nthawi yayikulu.” Akazi, vinyo, ndi nthawi yayikulu, iye amaganiza kuti akupitirira. Iye adzafa, iye adzalowa mnyanja yamoto ndi miyala ya sulfure yomwe

imayaka, kumene kuyaka kukuchitika kwa nthawi ndi nthawi, ndipo mwinamwake kwa zaka handiredi milioni moyo wake ukhoza kuzunzidwa mu nyanja ya moto ndi sulfure.

²³⁸ Ine . . . Inu mukuti, “Kodi uwo udzangokhala ngati mwala wa sulfure wa wamba?” Ine ndikukhulupirira kuti izo zidzakhala zoyipa kuchulukitsa ka milioni kuposa zimenezo. Ine ndikukhulupirira inu simungakhoze kufotokoza izo ndi moto, ndi moto weniweni. Chifukwa chokhacho chimene izo zayikidwa “ndi moto,” moto umenewo ndi chinthu chonyeketsa kwambiri chomwe ife tiri nacho. Iwo mwamtheradi umanyeketsa ndi kuwononga chirichonse, moto umatero. Chabwino, ndiye, izo zidzakhala mmenemo, koma inu mudzakhala ndi solo imene ukuyenera kuti idzalangidwe kudzera mu mtundu wina . . .

²³⁹ Tsopano, inu mukuyenera kusamalitsa mawu akuti *moto*, chifukwa Mzimu Woyera umagwiritsidwa ntchito “Mzimu Woyera ndi moto”; chifukwa moto wa Mzimu Woyera umawotcha tchimo, mwaona, ndipo umayeretsa.

²⁴⁰ Koma moto *uwu*, iwo ukuchokera ku gehena, ilo linati “nyanja ya moto.” Ndipo chirichonse chimene icho chiri, ndi chilango chowawa. Munthu wolemerayo anakweza maso ake, ali mu gehena, ndipo anati, “Mtumizeni Lazaro ndi madzi pang’ono pa zala zake, kuti adzandiyike pa milomo yanga, pakuti malawi awa akundizunza ine.” Musamaganize kuti kulibeko gehena woyaka, ndi gehena weniweni, kumeneko. Ngati alipo mdierekezi weniweni, gehena weniweni aliponso.

²⁴¹ Koma, inu mwaona, chirichonse chimene chinapotozedwa chiri ndi mathero ake, chifukwa izo potsiriza zikuyenera kubwerera ku chiyero ndi chiyero cha Mulungu. Ndipo Mulungu ndi Wamuyaya; ndipo ngati ife tiri ndi Moyo Wamuyaya, Mulungu ali mwa ife, ndipo ife sitingafe monganso Mulungu sangakhoze kufa. Ndi inu apo.

²⁴² Tsopano, mutuwo ukudzifotokoza Wokha kwenikweni, mwaona, ndi kuwupanga iwo kulondola. Tsopano, tiyeni tiwone, ine ndinali ndi . . . sindikudziwa ngati . . . Inde:

“Ndi chiyani—ndi chiyani chidzachitike kwa iwo?”

²⁴³ Iwo adzatha, sipadzakhalanso kanthu kwa iwo: solo imapita, mzimu umapita, moyo umapita, thupi limapita, malingaliro amapita, kukumbukira kumapita.

²⁴⁴ Ndipo sikudzakhalanso malingaliro oyipa, kapena iwo konse, adzakachitike konse, mu Ulemelero. Uko nkulondola, izo zonse zidzakhala . . . Kodi inu mungalingalire, kuti kudzakhala anthu cha kuno mu kawo ili . . . ?

²⁴⁵ Kodi Baibulo silinena kuti, “Ngakhale malingaliro a oyipa adzatatayika”? Malingaliro omwe a izo adzawonongeka.

²⁴⁶ Apa padzakhala munthu cha *apa*, apa pali Mulungu Woyerayo Wamkulu Uyo *apa*, ndipo nkumadziwa kuti cha uko

kuli dzenje limene masolo akuyaka kumeneko? Bwanji, uko sikungakhale Kumwamba. Malingaliro omwewo, kukumbukira komweko, chirichonse chimene chinapotozedwa, ganizo loyipa lirilonse, chirichonse chidzawonongeka, ndi chirichonse chimene chiri choyipa mmenemo. Ndipo ife sitidzakhala kalikonse koma chiyero, ndi Zoe, Moyo wa Mulungu; ku Muyaya, ndipo kwa mibadwo ikupitirirabe, ndi kupitirira, ndi kupitirira, ndi kupitirira, ndi kupitirira; Iwo sudzatha, udzakhala Wamuyaya!

²⁴⁷ “Iwo anapita ku chilango *chosatha*, koma olungama anakalowa ku Moyo Wamuyaya.” Inu mukumvetsa zimenezo? Chilango *chosatha*, Moyo Wamuyaya, ndi zosiyana bwanji!

²⁴⁸ Tsopano, taonani, izo sizitero. . . Tsopano, ine ndikudziwa, kwa inu, ana anga okondedwa, ine—ine sindikutanthauza kuyesa kudziwonetsera ndekha ngati wodziwa zonse. Ngati ndingachite zimenezo, . . .

²⁴⁹ Tsopano, ndiri ndi mafunso atatu kapena anayi abwino owonjezera. Ine ndidzawatenga iwo Lamlungu mmawa, Ambuye akalola.

²⁵⁰ Tsopano, penyani. Taonani, izi zimadzutsa mafunso. Ndine mlaliki wakale. Ine—ine—ine—ine ndiri ndi zaka twente-sikisi mu utumiki. Ndipo ine—ndine woyamikira kwambiri chifukwa cha izi, kuti ine ndikhoza kunena izi, mai. . . ine sindinayeserepo kuyesa kupereka chirichonse m'moyo wanga popanda icho kuwululidwa poyamba. Ndipo ndine wothokoza kwambiri kuti Mngelo wa Ambuye. . . Chimene ine ndinalibe maphunziro, ndinalibe kuthekera. Ndipo Mngelo uyu anatsika pansi, ndipo wakhala thandizo langa lotumizidwa kuchokera kwa Mulungu. Ndipo Iye sanayambe wandiuzapo chinthu chimodzi koma chimene mwamtheradi chinalumikizana kuchokera ku Genesis mpaka ku Chivumbulutso ndi zimenezo, mochuluka mpaka. . . Ine ndinalimba pansi mwamsanga pamene Iye anati “Ndipo iwe—ndipo iwe udzatenga mphatso ya machiritso Auzimu.” Ndipo ine ndinazilemba izo momwe Iye anazinenera izo.

²⁵¹ Ndipo pafupifupi zaka zitatu zitadutsa, manejala anayitanira changa—chidwi changa kwa izo, anati, “M'bale Branham, kodi inu munazindikira izo? Izo ndi zangwiro kwambiri mpaka Iye anakuuzani inu ‘mphatso.’”

²⁵² Mwaona, sananene konse “mphatsoyo.” Ndipo aliyense—aliyense mu Baibulo. . . mphatso iliyonse ndi “mphatso” koma machiritso Auzimu, ndipo iwo ndi “mphatso.” Ndi “mphatso za machiritso.” Inu mukhoza kukhala ndi mitundu yonse ya mphatso za machiritso, njira zosiyanasiyana. Koma, wina aliyense ndi “mphatso”: “ka” mphatso ka uneneri, “ka” mphatso ka *ichi*. Koma machiritso Auzimu ali mu zochuluka: “mphatso.” Ndipo ine sindinazindikire izo, kuti Mzimu Woyera ndi wangwiro kwambiri. Oh, adalitsike Ambuye!

²⁵³ Kodi inu mukumvetsa kuti Mzimu Woyera womwewo umene unalemba Baibulo limenelo, ndi mahandirede a amuna, mahandirede a zaka motalikana . . . ndipo palibe mmodzi wa iwo anapatukana wina kwa mzake, mmodzi aliyense wa iwo anali wamphumphu; ndipo mmodzi sanamve nkomwe za mzake.

²⁵⁴ Ndipo Paulo anapita kumeneko, ndipo anali uko mu Arabia, ndipo sanapite nkomwe ku Yerusalemu kwa zaka fortini, koma anali uko mu Yerusalemu ndi kumusi . . . anapita kuchokera . . . sanapite konse ku Yerusalemu. Koma anapita ku Arabia, ndipo anayamba kulalikirira, sanamuwone nkomwe Petro ndi ena onse a iwo kwa zaka fortini. Ndipo pamene iwo anabwera pamodzi, iwo anali akulalikira chinthu chomwecho: ubatizo wa madzi mu Dzina la Yesu Khristu, ndi machiritso Auzimu, ndi mphamvu ya Mulungu.

Oh!

Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena kuti
ndine mmodzi wa iwo.

Mmodzi wa iwo, ndine mmodzi wa iwo,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena kuti
ndine mmodzi wa iwo; (Aleluya!)

Mmodzi wa iwo, ndine mmodzi wa iwo,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena kuti
ndine mmodzi wa iwo.

Kuli anthu pafupifupi kulikonse,
Amenе mitima yawo yonse ikuyaka moto,
Ndi Moto uwu umene unagwa pa Pentekoste,
Umene unawayeretsa ndi kuwapanga iwo
oyera;

Oh, Iwo ukuyaka tsopano mkati mwa mtima
wanga,

Oh, ulemelero ku Dzina Lake!

Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena kuti
ndine mmodzi wa iwo.

Anasonkhana m'chipinda cha pamwamba,
Onse akupemphera mu Dzina Lake,
Iwo anabatizidwa ndi Mzimu Woyera,
Ndipo mphamvu yotumikira inadza;
Tsopano chimene Iye anawachitira iwo tsiku
limenelo

Iye achita kwa inu chomwecho,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena kuti
ndine mmodzi wa iwo.

Ndine mmodzi wa iwo, ndine mmodzi wa iwo,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena kuti
ndine mmodzi wa iwo; (Aleluya!)

Mmodzi wa iwo, mmodzi wa iwo,

Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena kuti
ndine mmodzi wa iwo.

- 255 Tamverani, ndiri ndi uthenga wapang'ono kwa inu:
Bwera, m'bale wanga, funa mdalitso uwu
Umene udzayeretse mtima wako ku tchimo,
Umene udzayambitse mabelu achimwemwe
kulira
Ndipo udzasiya moyo wako pa moto;
Oh, ukuyaka mkati mwa mtima wanga,
Oh, ulemelero ku dzina Lake,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena kuti
ndine mmodzi wa iwo.
- 256 Kodi sindinu okondwa kuti ndinu mmodzi wa iwo?
Icho ndi chiyani? Ndi Mzimu umene umawulula. Ndi
vumbulutso la Mulungu, "Pa thanthwe ili." Sindikusamala
ngati arkibishopu. . .
- 257 Wansembe wa Chikatolika anakhala, osati kale, mnyumba
mwanga. Ndipo iye anati, "Bambo Branham, ine ndabwera kuti
ndidzakufunsemi inu funso."
Ine ndinati, "Chabwino, bwana."
- 258 Anati, "Ine ndiri ndi kalata pano yochokera kwa bishopu,
yopita kwa inu."
Ine ndinati, "Chabwino, bwana."
- 259 Iye anati, "Maneno omwe inu mumapanga, inu mungagwire
dzanja lanu ndikulumbira kuti mumanena zoon?"
- 260 Ine ndinati, "Ine sinditero." Ine ndinati, "Baibulo linati,
'Musalumbire konse, kuchula miyamba kapena dziko lapansi
(pakuti ndi popondapo mapazi Ake). Mulole inde wanu akhale
ayi ndi inde.' Ngati bishopu akufuna kumva chimene ine
ndikuyenera kunena, iye atenga mawu anga pa izo. Ngati iye
satero, ine sindilumbira."
- 261 Wansembe wamng'ono uyu kuno ku mpingo wa Sacred
Heart, iye anati, "Kodi inu munamubatiza Pauline Frazier pa
tsiku *lakuti-lakuti*?"
- 262 Ine ndinati, "Ine ndinatero, bwana, kumusi mu Mtsinje wa
Ohio."
- 263 Anati, "Inu munamubatiza iye motani?"
- 264 Ine ndinati, "Ine ndinamubatiza iye pomumiza iye pansu
mmadzi mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu."
- 265 Iye anzilemba izo. Anati, "Inu mukudziwa, mpingo wa
Katolika unkabatiza monga choncho."
Ine ndinati, "Liti?"
Iye anati, "Mu zaka zoyambirira."
Ine ndinati, "Zaka zoyambirira ziti?"

Iye anati, “Chabwino, pachiyambi.”

Ine ndinati, “Chiyambi chake chiti?”

Iye anati, “Mu Baibulo.”

Ine ndinati, “Inu mukutanthauza a-. . .mu—mwa ophunzira?”

Iye anati, “Ndithudi.”

Ine ndinati, “Kodi inu mumawatcha Akatolika, kapena, a—. . .? Inu mumati ophunzirawo anali Akatolika?”

Iye anati, “Ndithudi, iwo anali.”

Ine ndinati, “Ine ndimagaliza kuti mpingo wa Katolika sunasinthe?”

Iye anati, “Iwo sutero.”

266 Ine ndinati, “Ndiye nchifukwa chiyani Petro anati, ‘Lapani, ndipo batizidwani mu Dzina la Yesu Khristu’? Ndipo inu mukuti izo zinali. . .kuti iye anali papa?”

267 “Eya.”

268 “Ndiye nchifukwa chiyani inu mumabatiza mu dzina la ‘Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera’? Ndipo iye anamiza, ndipo inu munakonkha. Tsopano chinachitika ndi chiyani?”

269 Iye anati, “Koma, inu mwaona,” anati, “mpingo wa Katolika uli ndi mphamvu yochita chirichonse chimene iwo akufuna kuchita.” Huh.

270 Ine ndinati, “Ndipo inu munawatcha ophunzirawo Akatolika?”

271 Iye anati, “Eya.”

272 Ine ndinati, “Bwana, ndiri ndi, Josephus, ndiri ndi *Foxe’s Book of Martyrs*, Ndiri ndi *Early Ages* ya Pember, ndiri ndi la Hislop *Two Babylons*, mbirizakale kwambiri zomwe ziripo padziko lapansi, ndiwonetseni ine mmenemo pamene mpingo wa Katolika unayamba wadzozedwapo kapena unabwera konse mu bungwe. . .zaka sikisi handirede itatha imfa ya mtumwi wotsiriza.”

“Oh,” iye anati, “ife timakhulupirira zomwe mpingo umanena.”

Ine ndinati, “Ndimakhulupirira chimene Baibulo limanena.” Mukuona?

“Bwanji,” iye anati, “Mulungu amakhala mu mpingo Wake.”

273 Ine ndinati, “Mulungu amakhala mu Mawu Ake.” Ndipo ine ndinati, “Ngati. . .” Iye anati. . .Ine ndinati, “Baibulo silimanena kuti Mulungu amakhala mu mpingo Wake, koma Baibulo limanena kuti Mulungu amakhala mu Mawu Ake. ‘Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu; ndipo anadzakhala pakati pathu.’”

Uko nkulondola. Ine ndinati, “Mulungu amakhala mu Mawu Ake.”

²⁷⁴ Iye anapitirira ndipo anakanena zimenezo. Iye anati, “Chabwino, ife sitingatsutsane,” anati, “chifukwa inu mumakhulupirira mu Baibulo, ine ndimakhulupirira mu mpingo.”

²⁷⁵ Ine ndinati, “Ine ndimakhulupirira kuti Baibulo ndi Mawu odzodzedwa a Mulungu ndipo mulibemo kutsutsana kumodzi mwa Ilo. Ndipo Ilo ndi Mawu a Mulungu, mapulani Ake Amuyaya a mibadwo yonse ikudzayi. Iye anati, ‘Miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka koma Mawu Anga sadzachoka. Uko nkulondola. Ine ndimawakhulupirira Mawu.’”

²⁷⁶ Iye anapita kwa Akazi a Frazier. Iye anati, “Akazi a Frazier, kodi inu mungasayine pepala apa lovomereza kuti mtsikana wanu akhale membala wa tchalitchi cha Katolika?”

²⁷⁷ Iye anati, “Kulibwino ine ndiyende naye kupita kumanda.”

²⁷⁸ Anati, “Manyazi pa inu.” Anati, “Inu mukuyenera kukhala wothokoza kuti mtsikana ameneyo akutuluka mu zamkutu zimenezo, akulowa mu mpingo wa Katolika.”

²⁷⁹ Anati, “Bwanji ngati ukanakhala iwe mtsikana ukubwera ku tchalitchi changa, unganene chiyani za izo?”

²⁸⁰ “Oh,” iye anati, “izo ndizosiyana.”

²⁸¹ Anati, “Ayi, izo siziri.” Iye ankadziwa kuti iye anali kwinakwake pamene iye anamusiya mkazi wamng’ono uja kunja uko. Iye ankadziwa kuti iye anali ali kwinakwake. Iye anati, “Tsopano, khomo lomwelo ndi lotseguka limene inu munalowera.”

²⁸² Mwaona, njira yake ndi imeneyo. Osamaponderezedwa, inu simusowa kuponderezedwa. Ngati Mulungu ali ndi inu, ndani amene angakutsutseni inu? Kulondola! Vuto la izo ndi lero, inu muli ndi nsana wa mbalame mmalo mwa nsana wa munthu. Mudziyima kumbali ya Mulungu ndiponso molondola!

²⁸³ Mzimu Woyera womwewo umene unatsikira pa atumwi amenewo ndi mmbuyo mmibadwo, ukadali mu Mpingo Wake lero, iwo amene Mulungu wadziululirako Yekha. “Osati iye amene afuna, kapena iye amene athamanga, koma Mulungu amene asonyeza chifundo.” Ndi Mulungu, mwa kusankha Kwake, amawabweretsa anthu ndi kuwatsegula maso awo. Inu simungakhoze konse kuwona Iwo, ndinu akhungu, ndipo simungawone nkomwe pokhapokha Mulungu atatsegula kumvetsa kwanu. Baibulo linati ndinu akhungu, ndipo inu simungathe kuwona. Palibe chifukwa choti muziyesera. Ndi maphunziro onse, maphunziro omwe mungakhale nawo, mumangochita khungu mosalekeza.

²⁸⁴ Tsopano, inu Mpingo wa Khristu pano, inu “mumalankhula pomwe Baibulo lalankhula, ndi kukhala chete pamene kuli

chete,” nanga bwanji zina mwa Izi? Inu muli chete kwambiri pa Izo. Kulondola.

²⁸⁵ Mwaona, zimatengera Choonadi chowululidwa mwauzimu. Kenako Mulungu amatsika pansu ndi kudzadzulula Yekha ndi kutsimikizira Izo kuti ndi Choonadi. Ameni! Inu mumamukonda Iye? Inenso ndimatero. Ameni.

²⁸⁶ Chabwino, nonse inu Amethodisti mukufuna kugwirana chanza ndi Abaptisti tsopano? Inu Apresbateria?

²⁸⁷ “Tsopano,” inu mukuti, “M’bale Branham, kodi inu mumawachotsa mu chiyanjano Abaptisti ndi Apresbateria amene samabati- . . .?”

²⁸⁸ Ayi, bwana, ine sinditero. Ndimawatenga iwo ngati abale anga. Mwamtheradi! Ine sindisamala ngati simunabatizidwe nkomwe, ngati inu munabatizidwa mu dzina la “Duwa la Sharoni, Kakombo wa Mchigwa, ndi Nyenyezi ya Mmawa,” izo sizikanakhala. . . izo zingakhale zabwino basi monga “Atate, Mwana, Mzimu Woyera.” Maudindo atatu okha. Iye anali Duwa la Sharoni. Kodi Iye anali? Kakombo wa Mchigwa, Nyenyezi ya Mmawa, zonsezo. Ndithudi, Iye anali. Chinthu chimodzi chokha kapena chimzake. Koma ndi ichi chimene icho chiri: njira yolondola ya Lemba ndi mu Dzina la Yesu Khristu. Ngati inu mukufuna njira ya Lemba, ndizo ndendende. Ndiyo njira yolondola.

²⁸⁹ Tsopano, ngati inu munabatizidwa mu dzina la “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,” ndikumverera ngati izo ziri bwino, ameni. Ngati ilo liri yankho labwino kwa Mulungu ku chikumbumtima choyera kwa Mulungu, ameni. Zipitirirani nazo, mwaona.

²⁹⁰ Koma monga momwe ndikudziwira, monga mwa gawo langa, ngati inu mukanati mundifunse ine, kuti, “M’bale Branham, kodi ine ndibatizidwense?” Ine ndikanati, “Inde,” gawo langa.

²⁹¹ Mkazi wamng’onooyo anabwera kuno tsiku lina, anati, “Ambuye anandiitana ine kuti ndidzakhale mlaliki.” Ine sindinazikhulupirire zimenezo, osati kuposa momwe ine ndikanakhulupirira kuti—kuti akhoza kulumpha pamwamba pa mwezi. Ndipo iye. . .

²⁹² Ine ndinati, “Chabwino, izo nzabwino kwambiri, mlongo.” Ine ndinati, “Kodi ndiwe wokwatiwa?”

“Inde.”

“Uli ndi ana awiri?”

“Inde.”

Ine ndinati, “Ndi chiyani. . .? Kodi mwamuna wako anapulumutsidwa?”

“Ayi.”

Ine ndinati, “Iwe uchita chiyani ndi iye?”

“Ndimusiya iye kunyumba.”

²⁹³ Ine ndinati, “Imeneyo ndi nyambo yabwino kwambiri imene mdierekezi anakhalapo nayo. Ndiwe mkazi wokongola kuyamba ndi kuyamba, ndipo iwe ukuzembera kunja kuno mmunda, iwe udzakhala nyambo yachizolowezi komanso chandamale cha mdierekezi. Ndipo mwamuna wako, kwanu, mnyamata, ndipo iwe umusiya iye ndi ana awiri awa; iye adzayamba kumayenda ndi mkazi wina, ndipo ana awa adzakhala ndi adadi ena limodzi la masiku awa.” Ine ndinati, “Malo oyambirira, ngati Mulungu anamuyitana mkazi, Iye anadzitsutsa Mawu Ake.” Ine ndinati, “Tsopano, ngati iwe ukufuna kutero, izo ziri bwino.” Ine ndinati, “Tsopano, kuzindikira za mu mtima, iwe ukuti Ambuye anakupatsa iwe kuzindikira za mu mtima. Kodi ukufuna kupita pamenepo, pa nsanja, ndi kukayesera izo?”

²⁹⁴ Iye anati, “Inde.” Ndikuwona chimene chingachitike.

²⁹⁵ Inu mwaona, ndi kutengeka. Izo zikuyenera kubwera ku Mawu. Ngati izo siziri mu Mawu, ndiye kuti si zolondola. Ine sindikusamala chimene zotengeka zanu ziri, izo sizoon. Ameni! Zimenezo zikumveka bwino. Ameni!

²⁹⁶ Chabwino:

Tiyenda mu Kuwala, Kuwala kokongola,
Kumabwera kumene mame achifundo
akuwala;

Kuwale motizungulira ife usana ndi usiku,
Yesu, Kuwala kwa dziko.

Oyera mtima onse a Kuwala lengezani,
Yesu, Kuwala kwa dziko;
Kenako mabelu Akumwamba adzalira,
Yesu, Kuwala kwa dziko.

Tiyende mu kuwala, kuwala kokongola,
Kumabwera kumene mame . . .
Kuwale motizungulira ife usana ndi usiku,
Yesu, Kuwala kwa . . .

²⁹⁷ Tsopano ine ndikufuna aliyense atembenuke ndi kugwirana chanza, mbali zinai, ndi aliyense tsopano, pamene ife tikuiyimbanso iyi:

Tiyende mu Kuwala, Kuwala kokongola,
(Ameni!)

Kumabwera kumene mame achifundo
akuwala;

Kuwale motizungulira ife usana ndi usiku,
Yesu, Kuwala kwa . . .

²⁹⁸ Kodi mmawakonda Amethodisti? Nenani, “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Abaptisti? Apresbateria?

Akatolika? A...oh, kodi mumawakonda iwo onse? Nenani, “Ameni.” [“Ameni.”]

Tiyende mu Kuwala, kokongola . . .

Tizigwirana chanza, pamene tikupita.

Oh, kumabwera kumene mame achifundo
akuwala;

Kuwale motizungulira ife usana ndi usiku,
Yesu, Kuwala kwa . . .

²⁹⁹ Tisanayimbe nyimbo yathu yobalalikira . . . Tsopano, ndizotheka kuti ndidzakhalanso pano Lamlungu. Tsopano, zikatha izo ine sindidzabwereranso mpaka itadutsa Khrisimasi. Mwaona, chifukwa ine ndikupita ku Michigan, kuchokera ku Michigan ndidzapita ku Colorado, kuchokera ku Colorado mpaka ku Idaho, kuchokera ku Idaho mpaka ku California, ndipo tizidzabwerera. Ndipo ndizotheka (ndikufuna kuti mundipempherere ine) ine ndidzakhala ku Waterloo, Iowa, kuyambira Januware twente-foro mpaka Feburuware thuu. Mwaona, bwalo lalikulu lija uko, ine ndangoyitanidwa kumene kanthawi kapitako, ndipo ine ndiri nazo kuchokera pano mpaka Lamlungu kuti ndipemphere. Mwaona, ku Waterloo, Iowa, komwe ndi pafupi tsopano.

³⁰⁰ Koma tsopano, mukumbukire, kukamvetsera kuwulutsa kwa m’baleyo pa naini koloko, Loweruka m’mawa. Ife tidzamuimbira iye ndi kudzamudziwitsa iye. Ndipo zimenezo zidzakhala pa WLRP, oyimba anayi a Neville pa naini koloko, Loweruka mmawa. Ife tidza . . . Ngati ine—ine sindidzawatenga iwo, M’bale Neville adzamalizitsa mafunsowo. Kodi mudzatera, M’bale Neville, Lamlungu mmawa? [M’bale Neville akuseka ndipo akuti, “Kulamula kwakukulu!”—Mkonzi]. Chabwino, onani, ngati mutalowa mu vuto, ndidzathamanga ndi inu. Iye adzayang’ana. Chabwino.

³⁰¹ Chabwino:

Tenga Dzina la Yesu nawe,
Mwana wachisoni ndi watsoka;
Lidzakusangalatsa ndi kukutonhoza,
Oh, litenge ilo kulikonse kumene upita.

Dzina lofunika, O ndi lokoma bwanji!
Chiyembekezo cha dziko ndi chimwemwe cha
Kumwamba;
Dzina lofunika, (Dzina Lofunika!) O ndi
lokoma bwanji! (Lokoma bwanji!)
Chiyembekezo cha dziko ndi chimwemwe cha
Kumwamba.

³⁰² Tsopano, ngati inu mukufuna kumudziwa wa Baptisti amene amakhulupirira mu kufuula, ndiwo mtundu wa kufuula umene ine ndimakhulupiriramo. Mayi wokalamba

uja wakhala pamenepoyo, ndipo Mzimu unadza pa iye. Iye anayamba kufuula, sanathe kuzigwira izo, anabwerera ndi kudzamukumbatira mwana wake wamkazi. Umo ndi momwe ndimakondera kuziwonera izo. Ameni. Ndizo zabwino kwenikweni, zakachitidwe kachikale, kumverera kokhudza mtima. Oh, mai, wokalamba—wokalamba, wokhwima, woyera wokhwima, wokonzeka kupita kwawo ku Ulemelero. Akungoyembekezera kuitanidwa, inu mwaona, akungokhala ndi nthawi yodabwitsa.

Chabwino, M'bale Neville tsopano, chirichonse chimene iye akufuna kuti achite. 🐦

57-0925 Mafunso Ndi Mayankho Ahebri Gawo I
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org